


Khwalala Ndiro Chipata

 Zikomo inu, M'bale Neville. Zikomo inu. Ndi chabwino kwambiri kukhala titabwerera mu Nyumba ya Ambuye. Ine nthawizonse ndimasangalala kubwereranso ku kachisi, ziribe kanthu kulikonse kumene ine ndipita. Pali chinachake za malo aang'ono akale awa kuti ine ndimakonda kubwererakonso. Ndiwo basi, o, ine... Iwo unali woyamba wanga ndi mpingo wokhawo umene ine ndachitapo konse ubusa. Ndipo izo zimangowoneka zabwino kubwereranso kuno kachiwiri. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti pa mmawa waukulu uwo pamene dzuwa likukana kuti liwale ndi nyenyezi kuziralitsa kuwala kwawo, ine ndikukhulupirira kuti adzakhalapo ena ochokera ku kachisi uyu alipo pamenepo tsiku limenelo, amene anatsukidwa mu Magazi a Mwanawankhosa. Ine ndikuyang'anira nthawi imeneyo.

² Pamene ine ndimabwera kudutsa mu chipinda tsopano pompa, ine ndinakomana ndi Mlongo Arganbright kumbuyo uko. Ndipo iye anali kundiuza ine kuti panali anthu ena pano amene anali ku msonkhano wa ku Kingston, amene anadzacheza pa nthawi imeneyo, ndipo ine... a... wokondwa kwambiri kukhala nawo iwo monga umboni. Paliponse pamene iwo ali, ngati iwo angakwezere manja awo mmwamba, anali ku msonkhano wa ku Kingston mu Jamaica. Basi, eya, mmbuyo kumbuyoko. Chabwino, ndizo zabwino.

³ Ine ndikuwona positi khadi ya Oral. Ine ndikuganiza inu mwalengeza kale misonkhano yake. Ine sindinayidziwe iyo mpaka, masiku, kufikira dzulo. Ine ndikuganiza iyo ikuyamba pa sikisi, sichoncho iyo? Sikisi mpaka pa fiftini, M'bale Roberts mu Louisville. Tsopano, pitani mukamumvere iye. M'bale Roberts ndi—mzanga wapachifuwa kwa ine, ndi wantchito weniweni wa Khristu. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu mukakondwera ndi mauthenga ake, usiku ndi usiku. Ndipo... yake, pamene iye akupempherera odwala, ine ndiri—ine ndiri wotsimikiza kuti inu mukamuwona Mulungu akusuntha, chifukwa iye ndi wankhondo wamkulu wa chikhulupiriro, M'bale Roberts ali, ndi mwamuna yemwe Mulungu akumugwiritsa ntchito mwamphamvu. Ndipo utumiki wake wakwera kuchokera...

⁴ Ine ndikukumbukira pamene ine ndinakomana naye koyamba M'bale Roberts, iye anali mu kahema kakang'ono kakutha uko mu St. Louis, Missouri, ndipo ine ndinali... ayi, Mzinda wa Kansas, Missouri. Ndipo ine ndinali mu Mzinda wa Kansas, Kansas, mu nyumba yoyankhuliramo. Iye anakhala pa mpando wa kutsogolo. Pamene msonkhano unali utatha, ife tinapita mozungulira kumbuyo ndipo anali kuyankhula.

Iwo anandidziwitsa ine kwa iye. Iye ndi wamng'onopo kuposa momwe ine ndiriri; Oral ali mu za makumi anai zoyambirira zake. Ndipo kotero iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti Mulungu angamve pemphero langa kwa odwala?”

Ine ndinati, “M'bale, Iye adzamvetsa pemphero la aliyense yemwe ati adzapemphere.”

Chabwino, iye anawuyamba kupita, ndipo iye anati, “Pano ine ndikupita!”

⁵ Ndipo iye ndi munthu wophunzira kwambiri, ndi maphunziro a ku koleji, zaka zinai za kuwerenga maganizo, ndipo ine ndikutsimikiza iye ali—iye ndi munthu waluntha. Ndipo iye wafika mpaka pa malo tsopano pamene iye ali nawo alangizi antchito pozungulira iye, ndi zinthu, mpaka, pamene iye ayankhula, iye—iye amaziganizira izo. Ndipo inu mudzasangalala naye iye kwenikweni, ine ndikutsimikiza.

⁶ Ndipo kotero tsopano ine ndikanafuna kuti ndipereke umboni pang'ono chabe pa zimene Ambuye wathu anachita mu msonkhano wathu wawung'ono wonyozeka mu Jamaica ndi mu Puerto Rico. Icho chinali chinthu chachirendo kuti ine ndinapita kumeneko, chifukwa kuyitana kochuluka kumabwera mkati. Monga Leo pano akudziwa, kuti foni . . . Ndipo kupyola mu kutha kwa sabata, pali kwenikweni malo mazana oyitanira misonkhano. Komabe ine ndimakonda kuti ndizimverera wotsogozedwa kumene ine ndikupita, monga kwa iwo. Ngati ine ndipita chifukwa chakuti munthuyo anatumiza kuti ine ndibwere, ndiye ine ndibwera mu dzina la mpingo umenewo kapena bungwe limenelo. Ngati ine ndikanati ndipite chifukwa M'bale Neville ananena kuti ine ndipite, ine ndikanakhala kuti ndipite mu dzina la M'bale Neville. Koma ine ndimakonda kuti ndipite pamene Yesu atuma, kotero inu mukhoza kupita mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti mukakumane nawo anthuwo.

⁷ Ndipo ine ndinali kugona pa kama, ndipo ine ndinakhala ndiri wotopa pang'ono. Chigwa ichi, posakhalitsa kapena mochedwerapo, ine ndiyenera kuti ndichoke ku chigwa ichi, chifukwa icho chikungomaswa mmero wanga mpaka pa malo oterowo kuti ine basi sindingakhoze mpang'ono pomwe kupirira izo. Ine ndikhoza kukhala nditachokapo ndi kukhala nditabwerera . . . Ife tinabwera tsiku lina, Leo ndi ine, mkati mwa mailosi makumi anai, pambuyo pa kukhala mu zithaphwi mu Florida, kummero conse kutayera, ndipo mkati mwa mailosi makumi anai a Louisville iko kunatchingika kachiwiri. M'bale Banks Woods ayenera kukhala pano penapake mmawa uno. Ndipo tsiku lina ndikubwera mkati kuchokera ku Kingston ndi—ndi Puerto Rico, kumene mmero wanga unali utangokhala uli wangwiro; ndipo ine ndinatsika ndege, ndikadali wabwinobe; ndipo ife tisanati tifike conse ku Jeffersonville, iko kunatchingika kachiwiri. Mukuona, ndi

chigwachi kuno. Ndi bakteria mu mpweya, kapena mwina ndi Mulungu, yemwe, akuyesera kuti andichotseko ine. Koteru, ine—ine sindikumvetsa izo. Ine ndapemphera ndipo ndafunsa nthawi zochuluka kwambiri.

⁸ Koma, ngakhale, ine ndinali nditangowuka, iwo unali pafupi firii koloko mmawa. Ndipo mkazi wanga ndi mnyamata wamng’ono anali akugona. Ndipo ine ndinawuka pa mbali ya kama, ndipo ine ndinawona chiwerengero chachikulu cha anthu amene anali atasonkhana pa malo aakulu, ndipo ine ndinati kwa Billy Paul, “Iwe upite mkati mmenemo ndi kukawapatsa anthu amenewo makadi a pemphero.”

⁹ Ndipo iye anati, “Chabwino, bambo.” Mu maminiti pang’ono iye anabwerera, ndipo anati, “Iwe sungakhoze kupereka makadi a pemphero kwa anthu amenewo.” Iye anati, “Inu mukumuwona munthu uyu wayima apayu?”

Ine ndinati, “Inde.”

¹⁰ Iye anati, “Iye anali cha kuno, ndipo ine ndinati, ‘Aliyense amene akufuna khadi la pemphero, ayimitse manja awo.’” Ndipo anati, “Ine ndinapita kukamupatsa iye khadi la pemphero, iye anapita kwinakwakenso. Ndiyeno ine ndinapita cha kumeneko, ndipo iye anali ali kwinakwakenso. Tsopano ndi uyu ali apa kumbuyo komwe cha kuno.” Anati, “Ine sindingakhoze ngakhale kupereka khadi limodzi la pemphero.”

¹¹ Ine ndinati, “Chabwino, Billy, iwe susowa kuti upereke makadi a pemphero, chifukwa pali danga lalikulu chotero pano mpaka aliyense akhoza...” Khadi la pemphero ndi loleta chiwawa...inu mukuona, ndi kuwasunga iwo mu dongosolo. Ine ndinati, “O, ine ndikhoza kumutenga aliyense pamenepo, mosachulukuka kuposa amene ali mu danga limene ine ndiri nalo, ndi kuwafuletsa iwo apo ndi kuwapempherera iwo mmodzi ndi mmodzi.”

¹² Ndipo iye anati, “Chabwino.” Ndipo iye anapotolokera cha kumanja ndi kupita kutali ndi ine. Ndipo ine ndinatembenukira mozungulira njira *iyi* pamene iye anali kupita njira *imeneyo*, basi kumangomuyang’ana iye.

¹³ Ndipo ine ndinamva Liwu likubwera pansu kuchokera Kumwamba, ndipo linati, “Koma pa nthawi *iyi* ine ndiyamba kukukulitsa iwe.” Ndipo ine ndinapenya, ndipo ine sindinayambe ndawonapo khamu loterolo la anthu, iwo anali piringupiringu kuchokera kulikonse.

¹⁴ Ndipo dzina la M’bale Roberts linatchulidwa, linati, “Tsopano M’bale Oral Roberts akubwera kuti adzakuwone iwe.”

Ndipo ine ndinati, “Ine ndidzamulonjera motani M’bale Roberts?”

Anati, “Basi momwemo momwe iye ati akakulonjere iwe.”

¹⁵ Chabwino, ine ndinamuwona M’bale Roberts akubwera atavala suti yakuda, ndi chipewa chaching’ono monga chimene Bing Crosby amavala, izo zazing’ono zotembenezidwa ndi kukokedwera pansi, kachipewa kakang’ono kakuda. Ndipo ine ndinali nditayima kukhala ngati pamwamba, ndipo iye anayang’ana mmwamba ndipo anati, “Moni, M’bale Branham.”

Ndipo ine ndinati, “Moni, M’bale Roberts,” ndinagwedeza dzanja lake.

Anati, “Iwe uli ndi unyinji wabwino.”

¹⁶ Ine ndinati, “Unyinji ndithu, M’bale Roberts.” Ndipo iye anatembenuka ndipo anachokapo momwe Billy anachitira, cha kumanja.

¹⁷ Ndipo ine ndinaganiza, “Kodi ine ndiyankhula kwa iwo kuchokera pati?” Ndipo ine ndinayesa paliponse kuti ndipeze malo woti ndiyankhulirepo. Ine ndinali mu chikhalidwe choterocho, chinachake pansi, mwakuti ine sindimakhoza kuwona poti—poti ndiyankhulirepo kwa iwo.

Ndipo winawake anati, “Chabwino, bwerani cha kuno.”

¹⁸ Ine ndinati, “Chabwino, iwe sukanakhoza kuwona bwinoko kumeneko.” Ndipo ine ndinayamba kudutsa pa malowo. Ndipo ine ndinakumbukira izi ndiye, ine ndinati, “Chinthu chachikulu choti ine ndichite ndi kukhalabe wodzichepetsa mu mtima wanga, nthawizonse, pamaso pa Mulungu ndi ana Ake.”

¹⁹ Ndipo ine ndinachoka mu masomphenyawo. Ndipo ine ndinaganiza, “Kodi zimenezo zikutanthauza chiyani? Mwinamwake izo zikutanthauza kuti ife tikakhala nazo zoterozo. . . Kapena ziri kuti izo, kodi iye akakhala ali kuti?” Inu mukuona, nthawizina, mu masomphenya, Iye samakuwuza iwe kungoti nkuti, Iye—Iye amangoyankhula ndipo iwe basi. . . Ziri mwa fanizo, monga. Ndipo ine ndikutsimikiza inu amene mumawerenga Baibulo mukumvetsa zimenezo.

²⁰ Ndiyeno ine ndinapita mu chipinda chakukhomo ndipo ndinakakhala pansi kwa kanthawi pang’ono, ndipo uwo unali pafupifupi hafu pasiti firii kapena foro koloko mmawa. Ine ndinakhala watulo kwenikweni. Ine ndinabwerera ndipo ndinakagona pansi, ndipo ine ndinalota loto, ndipo ilo linali loto losamvetseka kwambiri. Ndipo pafupi ambiri a nonse a inu mukumudziwa mmodzi wa mamananjala, Jack Moore, M’bale Jack Moore. Ine ndamudziwa iye kwa zaka. Ine ndimaganiza kuti ine ndinali kunjira kokacheza ndi mwana wawo wamkazi, msungwana wa pafupi usinkhu wa zaka khumi zisanu ndi ziwiri, ndipo ndinali nditamutenga iye pa dzanja, ndikumutsogolera iye chokwera phiri, Jackie wamng’ono. Chabwino, ine ndamudziwa iye kuyambira pamene iye anali chabe khanda loyamwa. Ndipo ine ndinali kumutsogolera iye chokwera phiri, ndipo ine ndinapita midadada itatu ya mu mzinda chokwera phiri, ndikumutsogolera msungwana uyu.

Ndipo ife tinabwera pansi pa mtengo wawukulu, ndipo iye anakhala pansi. Ndipo monga ochuluka a asungwana a zaka zopitirira khumi lero amavalira masiketi amenewo omwe, inu mukudziwa, okhala ngati otukumukira kunja, ndipo iye anali atavala mtundu wa masiketi amenewo. Ndipo iye anatenga siketi yaying'ono iyi ndi kukhala ngati kuyiyambakatitsa iyo apo ndi kukhala pansi. Ndipo monga anthu aang'ono nthawi zambiri amayang'anana pa wina ndi mzake, iye anapinda manja ake monga *chonchi* ndi kuyamba kumayang'ana mmwamba choloza ku mlengalenga. Chabwino, Jackie ndi msungwana wamng'ono wabwino kwambiri, koma iye ali ndi kamwa yayikulu kwambiri ndi maso aakulu kwambiri, ndi zokhala ngati tsitsi la mchenga, osati wokopa kwambiri, koma dona wamng'ono kwenikweni, ndipo ine ndimakhoza kuwaona maso ake aakulu pamene iye ankayang'ana choloza ku mlengalenga, ndipo momwe kunyezimira kwa mlengalenga kunali mu maso ake.

²¹ Chabwino, ine ndinapita pafupi mapazi asanu kuchokera kwa iye, ndipo ndinakhala ngati ndagona pansi cha mmbali monga *chonchi*, ndipo ndinapeza kaudzu ndi kukayika iko mkamwa mwanga, ndi kuyamba kutafuna pa kaudzu aka. Ndipo ine ndinayamba kuganiza, “Ine ndikuchita chiyani pamwamba pano? Bwanji, ine bambo wachikulire, ndipo ndi msungwana wamng'ono uyu. Bwanji,” Ine ndinati, “Ine ndine wokwatira ndipo ndiri nalo gulu la ana. Ine ndiribe ntchito iliyonse pamwamba pano ndi msungwana wamng'ono uyu.”

²² Ndipo ine ndinayamba kuti ndizinyamukapo. Ndipo, pamene ine ndinatero, Liwu linadza kuchokera mu mtengo, ndipo linati, “Izi ziri mwa chizindikiro ndi mwa chifukwa.”

²³ Ndipo ine ndinawukapo, ndipo ine pafupi ndikanafuula, ku—kubwebweta kutulo. Ine ndinaganiza, “O, ndikudabwa ngati izo zikutanthauza kuti ine ndidzabwerera mmbuyo kapena chinachake kuchitika kwa ine? Chabwino,” ine ndinaganiza, “ngati ine nditi ndiyese kuti ndigwiritse ntchito malingaliro anga omwe, ndiye ine ndifika pozisakaniza izo zonse, koteri ine ndingoyembekezera pa Mulungu.” Ndipo ine ndinayamba kupemphera. Ine ndinati, “Ambuye, kodi loto limenelo likugwirizana ndi masomphenya aja mu gawo loyambirira chabe la usiku, kapena kodi ilo likutanthauza chiyani?”

²⁴ Nditatha kuyembekezera nthawi yina, mwinamwake ora, (mkazi wanga anali atawuka kale ndipo anali atakonza kale kadzutsa), ndiye Liwu linabwereranso kachiwiri, ndipo linati, “Pitabe ku Kingston, ndipo zikawuzidwa kwa iwe kumeneko choti nkuchita.”

²⁵ Koteri, mwamsanga ine ndinapita ku Kingston. Ndipo iwo—iwo anadziwa Lachinai madzulo kuti ine ndikanakakhala kumeneko Lachisanu. Ndiko kulengeza konse kumene ife tinali nako. Ine sindiri wabwino kwambiri pa kupanga . . . ? . . . kapena

kuganizira maunyinjira, chifukwa ine kawirikawiri ndimasinjirira pa izo. Koma usiku woyamba, ine ndikananena kuti ife tinali nawo pafupi khumi ndi awiri, o, pafupi anthu mazana khumi ndi awiri, kunja, chifukwa iwo unangodziwika kwa tsiku limodzi lokha. Ndipo tsiku lotsatira iwo anayamba othamanga kuthamanga mailosi anai, pa kulandirana, kukwera mapiri. Wothamanga mmodzi amakhoza kuthamanga kwa maora anai, ndiyeno kumulola wothamanga wina kupitiriza pa phirilo. Ndipo usiku wachiwiri uko kunali pafupi zikwi zisanu. Ndipo usiku wachitatu iko kunaganiziridwa pozungulira zikwi khumi ndi zisanu, mwinamwake makumi awiri. Ndipo uko kunali zikwi kuchulukitsa zikwi anadza kwa Ambuye.

²⁶ Ndipo masomphenyawo, anali mpingo wawung'ono, msungwanayo anali namwali, mwana chabe, ndipo izo zimatanthauza unamwali wa mpingo. Ndipo midadada itatu ya mu mzinda chokwera phiri, anali masiku atatu amene ine ndikanatumikira. Ndipo kuwutenga mpingo wawung'ono waunamwaliwo mwa utumiki wanga, kuchokera kumene iwo unali, kuwuyika pamwambapo mu zinthu za Mulungu, mpaka iwo unagwedeza chisumbu chonsecho.

²⁷ Ndipo, o, atumiki ndi anthu kozungulira, akulira ndi kupempha ndi kuwumiriza, “Usiku wokha kapena uwiri woonjezera,” mabwana a mzinda.

²⁸ Ife tinapita kuchokera kumeneko ku Puerto Rico. Kumeneko ife tinakakumana ndi chachikulu, chisangalalo chapamwambako, ndipo zikwi kuchulukitsa zikwi anadzaza mu bwalo, mpaka iwo anaganiziridwa zikwi zina zina za miyoyo yofunika inadza kwa Ambuye Yesu. Ndipo pa kupita, ine ndikuyembekeza ine . . . ine ndikananena izi kwa mpingo wanga womwe, koma ine sindikanakhoza kuchita izo kunja mu chigulu, kuzungulira pamene anthu akwanu kulibe, chifukwa izo zikhoza kupenyedwa molakwika. Koma ine ndiri nalo dzina la woweruzayo pano pa chidutswa cha pepala, yemwe anapereka ndemanga pamene ife tinali kuchoka, pomwe pano, iye ndi gulu lake.

²⁹ Ndipo iye—iye anati, “Ife talemekedwa mu chisumbu kukhala nawo atumiki osiyana.” Iye anati, “Pamene Bambo Billy Graham angochoka pa chisumbu posakhaliitsapa,” ndipo anati, “ife tinali nawo m—msonkhano waulemerero,” iye anati, “koma Billy Graham anangotibweretsera ife Uthenga womwewo umene ife takhala tikuwumva nthawizonse.” Iye anati, “Ndiye ife tinalimekedwa kukhala ndi Bambo Roberts pa chisumbu,” iye anati, “ndipo Bambo Roberts anatipatsa ife msonkhano wawukulu wa masiku atatu. Koma,” anati, “zolipira zinali zokwera kwambiri mu hotelo,” anati, “anasiya madola zikwi makumi atatu ndi asanu kwa usiku utatu, zoti tilipire ku hotelo.” Iye anati, “Ndiye Bambo Osborn anali pano, yemwe anali wantchito wopambana wa Khristu. Koma,” anati, “pamene

Bambo Osborn anachoka, apo panali kusimidwa,” anati, “izo zimawoneka ngati chirichonse chinali chitapita.”

³⁰ “Koma,” anati, “ife tinazindikira mu msonkhano uwu kuti apo kwenikweni panalibe nkomwe aliyense pa nsanja kuti M’bale Branham amupempherere. Koma,” anati, “pamene misonkhano inali itatha, ife tinatolera zodzaza magalimoto ndi mipando yakale ndi ndodo ndi chirichonse, kunja pakati pa omvetsera.” Iye anati, “Uyo sanali munthu nthawi iyi, Mulungu anabwera kwa ife,” iye anatero.

³¹ Ine ndinati, “Musati muziyembekezera mapemphero anga; koma mapemphero anu kunja uko, sanjikani manja anu pa wina ndi mzake.” Ndipo iwo amabweretsa mwinamwake dazeni kapena awiri pa nsanja, ndipo, pamene kudziwa za mmitima kumabwera pansu, anthu anali akungofuula. Ife tinkakhala mu hotelo ya kalasi yachinai, ndipo tinalipira zogula zathu zomwe ndi maulendo, ifeeni.

³² Inu munathandizira kuchita zimenezo, inueni, ndi zachikhumi zanu zimene inu mumanditumizira ine. Ndizo zimene zinachita izo. Ndipo ine ndikufuna inu kuti mudziwe kuti, kuchokera mu izo zonse, inu muli nalo gawo la izo. Ndipo mu tsiku lalikulu laulemerero limene likudza, Mulungu adzakupatsani mphoto inu pa izo. Onani, inu simunachite kukhala . . .

³³ Ngati munthu mwiniwake apita ndi kukachita chinachake, ndiye, inu mukuona, pamene munthu ameneyo achoka, iwo amaganiza, “Kusiyidwa kwakukulu, Mulungu watisiya ife.” Mulungu samakusiyani inu. Iye ali ndi inu nthawizonse. Mwaona, ndi inuyo basi mwakuchuluka mu izo monga aliyense, monga aliyense. Mulungu akhoza kumugwiritsa ntchito munthu kwa utumiki winawake, koma izo sizikutanthauza kuti munthu ameneyo ali nacho chosankha pa Mulungu. Ndi chikhulupiriro chanu chomwe mwa Mulungu.

³⁴ Ndipo iwo amakhoza kupita kunja uko mu ngolo yaying’ono ya magudumu yachikale, imene iwo angatenge monga chikuku cha magudumu cha mwana, ndi—ndi kupanga bolodi, ndi kuwagoneka anthu pa iyo ndi kuwagudubuziramo iwo mkati. Ndipo utatha msonkhano, njira zonse za mjaha zitayeretsedwa, iwo amangopitirirabe ndi ngolo ndi kukokolola zazing’ono zachikale ndi mipando yayikulu yachikale, ndi ndodo ndi timakama ndi makama, ndipo basi kumene iwo anangoyenda kuchokapo ndipo anazisiya izo, chifukwa chakuti Kukhalapo kwa Ambuye kunali pamenepo. Ndicho chimene ife tikufuna kuchiwona. Munthu wachoka pa chithunzicho ndiye, Mulungu ali kusuntha.

³⁵ Pobwereranso, basi kuti tithandizire tsopano mmawa uno, ine ndati ndiyankhule mu maminiti pang’ono. Ndipo ine ndinawafunsa anyamata kuti asatulutse tepiyo. Masiku atatu ine

ndayesa zolimba kulingalira, “Ine ndikayankhula pa chiyani?” Ndipo mmawa uno, ine ndisanachoke, ine ndinamverera chenjezo lolimba kwenikweni mu mtima wanga kwa mpingo. Ndipo ine ndinawauza iwo, “Tengani tepi, koma musati muzitulutse izo kuti zigulitsidwe.”

³⁶ Koma ife tisanafike pochita izi, ine ndikanafuna kuti ndikupatseni inu umboni waung’ono chabe, kuti iwo mwina ungakuchitireni inu ubwino. Iwo unandichitira ine ubwino. Ife tinapita pa ulendo wa masiku atatu wokaweza, Leo ndi Gene ndi inemwini, ndi mwana wanga wamamuna Billy Paul ndi mkazi wake, uko kwa mzanga yemwe amabwera kunu ku kachisi, wochokera uko mu Georgia. Ndipo iwo ananitengeranso ife pobwerera mu chithaphwi china, ine sindikudziwa chabe kumene iko kunali tsopano, pafupi ndi Okeechobee kapena chinachake monga choncho, ine sindikudziwa dzina limene Amwenye achi Seminole awo analipatsa ilo. Koma, ngakhalebe, ife tinali mamailo ambiri pobwerera.

³⁷ Ndipo M’bale uyu Evans, m’bale wake ndi wochimwa. Ndipo iye ndi nsodzi wamkulu, ndipo iye anabworeranso mu zithaphwi miyezi ingapo yapitayo. Ndipo iwo ali nazo zimene iwo amazitcha “m’bobo wa pansu.” Ndipo m’bobo wa pansu unamuluma iye, ndipo iye anangokhala moyo mwapang’ono. Phazi lake linatupa, ndipo iwo anamutengera iye kwa madokotala ndipo iwo anamupatsa iye kubayidwa. Zinthu zimenezo ndi za kupha. Ndipo iwo ali ndi za kamwalathonje zochulukira kumeneko naponso, kamwalathonje, mphiri, ang’adzi ofika mpakana utali wa mapazi makumi awiri.

³⁸ Ndipo pamene ife tinali kuweza kumeneko, ine ndinali nditagwira nsomba yayikulu kwambiri. O, ilo linali tsiku lenileni la—la kupumula. Ndipo iyo inali yayikulu kwambiri ine sindikanakhoza kuyitulutsa iyo kuchokera mmadzimo, ndipo iyo inangowongola mbezayo ndipo inapitabe, kapena kudzikoka yokha momasula. Ndipo ife tinali nawo makanana ambiri, pafupi mapaundi zana ndi makamu asanu a makanana aakulu. Ndipo izo, zina za izo zolemera mapaundi angapo, ndipo ku chokera mapaundi anai mpaka asanu ndi awiri, asanu ndi atatu. Ndipo ine ndinakola imodzi yayikulu iyi, ndipo iyo inamasula.

³⁹ Ndipo ine ndinaponyeranso, ndipo ine—ine ndinakola imodzi ina, pafupifupi mapaundi asanu ndi imodzi, asanu ndi awiri. Ndipo ine ndinali ndi ndodo yayitali imene iwe umachita kuyigwira ndi ziyangoyango za kakombo. Ndipo M’bale Evans anali. . . Ife tinali tonse onyowa chifukwa choyenda mmadzi, chifukwa ndi kwa madambo basi. Ndipo iye anali atavula nsapato zake ndipo anakwinya miyendo ya thalauza lake, ndipo anali atakhala pa malo aang’ono owuma, kukhala ngati akuwumitsa zovala zake. Ndipo iye anayiwona nsomba yayikulu iyi ikusambira mozungulira mu tchire, ndipo ine ndinali kudutsa kumka kwa iye. Iye anati, “Miniti chabe,

M'bale Branham, ine ndikakutengerani inu iyo.” Ndipo iye anathamangira kumeneko. Ndipo ine ndinali nditayikoka iyo, ndikuganiza kuti nsombayo inali pafupi yophedwa, ili mu ziyangoyango. Ndipo iye anathamangira uko kuti akayitenge iyo. Ndipo, pamene iye anatero, iye anakuwa molira, ndipo pano iye anabwerera. M'bobo utamuluma iye.

⁴⁰ Ndipo ife tinayang'ana pa iwo, ndipo apo panali mabowo a dzino mu phazi lake pamene M'bobo unali utamumenya iye, ndi ilo linali kumupweteka iye moyipa kwambiri mpaka misonzi inali mu maso ake. Anati, anamverera ngati kuti mafupa ake anali akuchita zanzi basi. Ndipo apo ife tinali, mailosi ambiri kutali mu chithaphwi. Iye ndi mwamuna wamkulu kuti uchite kumunyamula. Ndipo pamene njoka ikuluma iwe, iwe umadwala kwambiri mu maminiti pang'ono mpaka iwe basi umakhala pafupi kufa. Ndipo Leo anali ali pamenepo atayima. Ndipo chinachake chinabwera pa malingaliro anga, “Inu mukadali Mulungu!” Ndipo pamene iye anali atagwira phazi lake ndi kuligwira ilo molimba, ndipo mabowo aakulu a dzino awo mmenemo pamene M'bobo unali utamumbwanda iye, ine ndinayika manja pa malo amenewo ndipo ndinati, “Ambuye, izo zalembedwa mu Mawu Anu, “Iwo adzaponda pa mitu ya njoka ndi zinkhanira, ndipo palibe kanthu kati kadzawavulaze iwo mulimonse.” Ndipo pa nthawi yomweyo, ululu uliwonse unasiya phazi lake. Anavala nsapato zake ndipo anaweza tsiku lonse.

⁴¹ Anapita mkati usiku umenewo ndipo anakawawuza iwo za zimenezo, iwo anati, “Iwe kulibwino kuti upite kwa dokotala.”

⁴² Iye anati, “Ngati Mulungu wanditeteza ine mpaka apa, Iye andisamalira ine njira yonseyo.” Ife tinaweza masiku atatu, popanda ululu wa kudwala konse.

⁴³ Mulungu panobe akadali Mulungu. Iye amasunga lonjezo lirilonse. Ndipo mwa utumiki wanga wonse, ndiyo nthawi yoyamba imene ine ndinayamba ndamuwonapo Mulungu atabwera pa kulumidwa ndi njoka, chifukwa iyo inali nthawi yoyamba imene ine ndinayamba ndakhalapo nawo mwayi kuti ndimupempherere winawake wolumidwa ndi njoka. Basi kungokulolani inu kudziwa kuti Iye amasunga malonjezo Ake onse, ndipo Mawu Ake ali abwino ndi owona. Amen.

⁴⁴ Kumbukirani misonkhano usikuuno ndi Lachitatu likubwerali. Ndipo pemphererani winawake tsopano yemwe akusowa kwenikweni kuti apemphereredwe, ameneyo ndi ine. Ndipo, kumbukirani, kukakhala pa msonkhano wa M'bale Roberts pamene iwo ubwera mu tawoni, ndipo kamulonjerani iye kuchokera ku Kachisi.

⁴⁵ Ife tisanati tiwerenge Malemba, ine—ine ndikanafuna kuti ife tiyime pa mapazi athu miniti yokha. Ndipo, popanda zing'wenyeng'wenye, tiyeni tingoyimba kolasi kapena ziwiri

za nyimbo yaulemerero yakale iyi ya mpingo, “Chikhulupiriro Changa Chikuyang’ana Mmwamba Kwa Inu.” Chabwino, aliyense alumikizane kumene ndi ine tsopano, ndipo tiyeni tiyimbe iyo. Ndipo musati muganizire za momwe inu mukuyimbira iyo, zingoyimbani iyo kwa ulemerero wa Mulungu. Kodi inu mungatipatse ife kutsogolera pa iyo, M’bale Neville?

Chikhulupiriro changa chimayang’ana kwa
Inu,
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi wauzimu;
Tsopano ndimvereni pamene ndikupemphera,
Tengerani kutali kulakwitsa kwanga konse,
O ndiroleni ine kuyambira tsiku lino
Ndikhale mwathunthu Wanu!

Pamene m’njira yokhotakhota moyo ine
ndiyendamo,
Ndi zokwiyitsa pozungulira ine zifalikira,
Khalani Inu Namulondola wanga;
Thamangitsani mdima utembenezikire ku
usana,
Pukutani chisoni, mantha zichoke,
Musati mundirole ine konse ndisochere
Kuchokera kwa Inu chakumbali.

⁴⁶ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikanafuna kuti ndiwerenge kuchokera mu zolembedwa zopatulika za Baibulo, Mateyu Woyera, mutu wa 7, ndime za 13 ndi 14. Ndipo mulole Ambuye awonjezere madalitso Awo olemera pamene ife tikuwerenga Izo.

*Lowani inu mkati pa chipata cha khwalala:
pakuti chotambalala ndicho chipata, ndipo njirayo
ndi yotakata, imene imatsogolera ku ziwonongeko,
ndipo ambiri kumeneko amakhalapo amene amapita
kumeneko nayo.*

*Chifukwa khwalala ndiro chipata, ndipo yopapatiza
ndiyo njira, imene imatsogolera kupita ku moyo, ndipo
apang’ono kumeneko amakhala amene amayipeza iyo.*

⁴⁷ Tiyeni ife tipemphere. O Mulungu, Amene munamubweretsa kachiwiri Ambuye Yesu kuchokera ku imfa ndi kuchokera ku manda, ndipo mwamupereka Iye kwa ife mmawa uno ngati Nsembe yamoyo, ife modzichepetsa tikupereka miyoyo yathu kwa Inu mwatsopano, pa malingaliro akuti Inu mukanakhala okumbukira chotero za ife. Pamene ife tinali tikadali ochimwa, akufa mu tchimo ndi zolakwitsa, Inu munamutuma Mwana Wanu yekhayo wobalidwa, wopangidwa mwa mawonekedwe a mnofu wochimwa, kuti akhale chitetezero cha machimo athu, kuti Wosalakwa, povutika chifukwa cha ochimwa, akakhoze kutiyanjanitsa ife palimodzi kachiwiri mu chiyanjano ndi Inu.

48 Ndipo, O Mulungu, ngati liripo tchimo pakati pathu mmawa uno, chinachake chimene chikanakhoza kutchinga Mzimu Woyera kuti utibweretsere ife Uthenga wa Mulungu kwa uliwonse wa mitima yathu, ife tikupemphera kuti, modzichepetsa, Ambuye, Inu mutikhulukire ife za zolakwitsa zathu. Tiyeretseni ife ndi Magazi a Ambuye Yesu. Yemwe ife tikumudziwa mwa ifeeni ife sindife kanthu, ndipo ife tikuvomereza kuti ife sindife kanthu, koma Inu muli woyera, Inu ndinu wona, Inu ndinu chilungamo, Inu ndinu Kasupe amene wa chifundo. Ndipo ife modzichepetsa tikukwawira kumeneko lero, ngati miyoyo yolapa. Monga umboni wapitira kumene posachedwapa, kuchokera ku Jamaica ndi kuchokera ku Puerto Rico, ndi kumene Inu mwachita ntchito zopambana choterozo, O Mulungu, ndicho chizindikiro cha kudza kwa Mmodzi Wolungamayo.

49 Momwe Inu munamuwombolera M'bale Evans kuchokera ku mano a chiphe cha njoka ija, chifukwa iye anali wokhulupirira, ndipo Mawu Anu ali nthawizonse owona. Tsopano, Ambuye, tiwomboleni ife ku mano a imfa mmawa uno, kumene mdani watiluma ndipo watipatsa ife chiphe. Mulole mankhwala Anu amachiritso, mmawa uno, Ambuye, alowerere mizimu yathu ndipo atitsuke ife ku kusalungama konse. Chizani matenda a matupi a mnofu amene aswekera pansu mwa mphamvu za mdani. Onse amene ali mu Kukhalapo Kwaumulungu, mulole iwo akhale ochiritsidwa.

50 Yankhulani kwa ife tsopano kupyolera mu Mawu Anu olembedwa, Ambuye. Posadziwa choti ndinene, koma Inu muchipereke icho. Ndipo Inu mutichenjeze ife, Ambuye, ndi kutipanga ife kukonzekera Kudza Kwanu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu ndi chifukwa cha Iye. Amen.

51 Ine nthawizonse ndimakhala wochedwerako pang'ono, chifukwa ine ndikuyembekezera tsopano. Ndipo Sande sukulu, ine ndikuganiza, iyo yatuluka. Koma pali chinachake za iyo, pamene ine ndibwera kwathu ine ndimangomverera ngati ine ndiri nayo nthawi yochuluka. Inu mukudziwa, ife tiri mu liwiro lochuluka kwambiri, mulimonse. Chotero, ife tingoyenera kuti tizimukhulupirira Mulungu.

52 Ambuye wathu anali kupereka chenjezo lolimba ili kwa anthu a m'badwo Wake, anthu amene anali achipembedzo kwambiri. Ndipo Iye anati, "Khwala ndiro chipata, ndipo njira ndi yopapatiza, imene imatsogolera ku Moyo, ndipo apang'ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze Iyo." Tsopano, izo sizinali chifukwa iwo sanali achipembedzo. Iwo anali achipembedzo kwambiri. Ndipo chifukwa chakuti iwo anali atadalira mu mpingo ndi mu tizikhulupiriro tinatake ndi zipembedzo, ndipo anali atakhulupirira (mpaka pakuti) mwa Mulungu, iwo ankaganiza kuti chirichonse chinali bwino bwino.

Koma Iye anali kuwauza iwo kuti pakanadzakhala ochepa amene akanati adzalowe mkati.

⁵³ Ndipo ine ndikudabwa mmawa uno ngati ine sindingakhoze kuwufanizira m’badwo umenewo kwa m’badwo uno. Onani, izo zinali pa kutseka kwa m’badwo wa Chiyuda, ndipo Iye anali kuwalozera mmbuyo ku yina yosiyana ndi mapeto osiyana a nyengo zosiyana, ndipo anali kuwauza iwo kuti chinthu chomwecho chimene chinachitidwa mu nyengo zakale chinali chikuchitidwa pamaso pa iwo. Ndipo iwo analephera kuti achizindikire icho. Ndipo tiyeni tiwone zina za zinthu zimene Iye anali kukamba za izo.

⁵⁴ Iwo, mwa chitsanzo, sakanakhoza kukhulupirira kuti Mulungu anali mwa Munthu ameneyo. Chimenecho chinali chopunthwitsa chachikulu kwambiri chimene iwo anali nacho kuti akwere pa icho, chinali momwe kuti Iye pokhala Munthu komabe ankadzipanga Iyeyekha kukhala Mulungu. Iwo sankakhoza kuwona momwe Mulungu akanakhoza kukhala mu mnofu wa umunthu. Ndipo mu mibadwo yonse, mu nthawi zonse, Mulungu anali nthawizonse akukhala mwa munthu. Munthu ndi chida cha Mulungu. Mu m’badwo uliwonse, Mulungu amayankhula kwa anthu ake kupyolera mu milomo ya umunthu. Iye nthawizonse amamusankha winawake kapena chinachake chimene Iye angakhoze kuchigwiritsa ntchito.

⁵⁵ Ndipo Iye analozera kwa iwo, ngati kukhala chopunthwitsa chotero, zokhudza Abrahamu. Iye anati, anawauza iwo, “Ngati inu mukudzitcha nokha ‘ana a Abrahamu,’ Abrahamu ‘atate’ wanu, iye anawona tsiku Langa ndipo anakondwera kuliwona ilo. Abrahamu, mneneri.” Ndipo ndi popanda kukaika kuti Yesu anali kulozera kwa iwo kuti Iye anali atatsimikizira kwa iwo kuti Iye anali Mesiya, chifukwa chizindikiro cha Mesiya chinali kumutsatira Iye. Ndipo izo zinali ziri mwa njira imeneyo kupyola mu m’badwo uliwonse, icho, chizindikiro cha Mesiya. Komabe Iye podzipanga Iyeyekha Mulungu, Mesiya Mwiniwake, izo zinawapunthwitsa iwo. Iwo sakanakhoza kuzimvetsa izo.

⁵⁶ Tsopano, pamene Abrahamu (yemwe iwo ankamutcha atate wawo) anakomana ndi Mulungu, Iye anali aponso mu thupi, chifukwa Iye anadya nyama ya ng’ombe, anadya mkate wa chimanga, ndi kumwa mkaka, ndi batara, mu kukhalapo kwa Abrahamu, ndipo komabe Iye anali Mulungu. Abrahamu anamuzindikira Iye, Mulungu, ndipo anamutcha Iye “Elohim,” chimene chiri Yehova Wamphamvuzonse. Munthu atavala zovala, ali ndi fumbi pa Thupi Lake, ndipo anakhala panso pa mtengo, kufuna mthunzi, ndi kumadya nyama ndi kumwa mkaka. Ndiye Ayuda awo ozizira, a mtima-wankhanza, awumbombo, achilungamo sakanakhoza kumukhulupirira Iye kuti angakhale Mwana wa Mulungu, ndipo ankamutcha Abrahamu atate wawo. Ndipo Iye anali kuwalola iwo kudziwa kuti Iye anali kuchita zinthu zomwezo, mu mnofu Wake, zimene

Mulungu anachita mu mnofu wina pamene Iye anakomana ndi atate wawo, Abrahamu. Ndipo Abrahamu anazikhulupirira izo. Ndipo iwo sankakhoza kukhulupirira izo.

⁵⁷ Inu mukuona, pamene Abrahamu anali atakhala pansi pa hema yake chifukwa iye anali atapanga kusankha, ndipo kusankha kumeneko kwabweretsedwa pamaso pa munthu aliyense yemwe wabadwa mu dziko lino. Mtengo wa zabwino ndi zoyipa wayikidwa pamaso pa munthu aliyense. Ndipo pamene Loti, mzukulu wake, ndi abusa awo anayamba kukanganira za malo; Abrahamu, pokhala munthu wolungama, ananena kwa iwo, “Mungolola kuti pakhale popanda makangano pakati pathu. Inu mungosankha njira yanu ya kopita.” Malo amenewo amabwera kwa moyo wa wokhulupirira aliyense. Ndipo ziri pamaso pa inu mmawa uno, ndipo ziri pamaso pa ine.

⁵⁸ Loti sanali kuganiza kuti iye anali kupita kukabwererammbuyo, koma iye anapita akuyang’ana cha ku Sodomu kumene zinthu zinali zophweka. Ndipo pali nthawi zambiri zimene ife timayang’ana cha ku njira yophweka. “Ine ndijowina mpingo uwu wakuti-wakuti, ndipo, inu mukuona, palibe yemwe ati anene chirichonse motsutsa izo, chifukwa ndi mpingo wawukulu kwambiri mu mzindawo.” Njira yophweka! Nthawi zambiri ife timachita zimenezo, pamene, ife tiri olakwitsa!

⁵⁹ Kumbukirani, ngati inu mutsatira Khristu, inu mudzakhala muli kudedwa ndi anthu, pakuti onse amene akhala mwaumulungu mwa Khristu Yesu adzasautsika nako kuzunzidwa. Ndipo ngati inu mubwera kwa Khristu, inu simudzabwera mwa mpingo uliwonse kapena chipembedzo chirichonse, kapena kachikhulupiriro kalikonse. Inu mudzabwera mwa Magazi, ndiyo njira yokhayo yoloweramo. Ndipo inu simungakhoze kumubweretsa mmodzi aliyense ndi inu, inu mudzabwera nokha ndi kuyima pa kuvomereza kwanu kwanu ndi chikhulupiriro chanu chanu. Inu simudzakwera pa abusa, kapena pa chikhulupiriro cha amayi anu. Inu mudzabwera ngati munthu payekha pamene inu mubwera kwa Mulungu! Ndipo nthawi zambiri ife timapanga kusankha kopusa kumeneko.

⁶⁰ Bwanji ngati Loti, pamene iye anawona chirichonse chophweka, iye anawona kumene kunali ndalama zochuluka ndi kuchuka kochuluka, chifukwa iye akanakakhala mlendo, ndi munthu wanzeru, wophunzira, kuwerenga maganizo kochuluka, ndipo iye akanakhoza kuchita zinthu zinazake ndipo komabe nkusunga chipembedzo chake. Iye anaganiza, “Ine ndiri nacho chikhulupiriro mwa Mulungu, kotero ine ndingopita kumusi kukalowa mu Sodomu ndipo ine—ine ndikapanga ndalama zina zapadera, ndipo ine ndikakhala munthu wotchuka, mwinamwake mlaliki wodabwitsa.” Mwaona, iwe uli nako kusankha kuti ukupange.

⁶¹ Ndipo amumpingo ali nako kusankha kuti akupange. “Ine ndipita uko ku mpingo winawake uwu. O, aliyense mu tawoni akuganiza kuti uwu ndi wopambana! Bwanji, ameya a mzinda ali mu mpingo umenewu.” Tsopano, iye akanakhoza kukhala wa mpingo umene unali wabwino kwenikweni, koma apabe iwe uyenera kuwuweruza mpingo umenewo ndi anthu ake mwa Malemba. Nthawizina iwo amapitako chifukwa ndiyo njira yotchuka, a—anthu amavala bwino amene amapita ku malo ena akewo. Ndipo apo ndi pamene ife timapanga ku—kulakwitsa kwangozi. Tsopano zindikirani izi.

⁶² Ndipo Abrahamu, chinthu chokha chimene iye akanakhoza kuchita chinali kutenga kusankha kwachiwiri. Ndipo nthawizina kusankha kwachiwiri ndi kwabwino kuposa koyamba, ngati iko kutengedwa monga choncho. Zindikirani, sikunali motalika, pamene Loti anawona mzinda wawukuluwo, iye sanamuwone mkazi wake akusandulika chulu cha mchere, ngakhale, iye sanawuwone moto ukuwutentha mzindawo. Koma Abrahamu anatenga njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye. Iye anakhala mu zipululu.

⁶³ Ndipo, komabe, bwanji ngati Sarah akanati anene... Tsopano kumbukirani, Sarah anali mkazi wokongoletsetsa mu dziko lonselo. Uko kunali kulibe mkazi wokongola monga Sarah. Aliyense, akamuwona iye, ankagwera mu chikondi ndi iye. Tsopano, zikanakhala zophweka motani kwa Sarah kuti atenge kusankha kwa mtundu umenewo. Koma iye anasankha kuti akhale ndi Abrahamu.

⁶⁴ O, akazi, musati mulole Mdierekezi akuchititseni inu khungu, pokhala otchuka ndi kujowina *izi* ndi *izo*. Inu mukhale ndi Khristu! Pakuti, ora liri pafupi, ziwonongeko zazikulu zagona patsogolo, zoyipitsitsa kuposa Sodomu ndi Gomora, kwa dziko ili. Sodomu ndi Gomora adzakhala wabwino kwa icho.

⁶⁵ Tsopano, pamene Abrahamu anali atatenga njira imene anapatsidwa iye ndi Mulungu, ndipo anali nako kowondetsetsa kwa dzikolo, iye sanali waulemerero konse. Komabe iye ankadziwa chinthu chimodzi, iye ankatumikira Mulungu ndipo iye ankamukhulupirira Mulungu.

⁶⁶ Kotero tsiku lina uko kunadza amuna atatu, ndipo iwo anali afumbi bwino ndi olema, ndipo Abrahamu anamvera chisoni pa iwo, iye anati, “Dzerani pano ndi kudzakhala pansi pansi pa mgwalangwa kwa kanthawi pang’ono chabe.” Ndipo pamene iye anali atayima pamenepo akuyankhula kwa iwo, iye anazindikira kuti iwo sanali chabe anthu wamba. Mwa kayankhulidwe kawo, iwo anali osiyana. Ndipo Abrahamu anapita ndipo anakapha mwana wa ng’ombe ndipo anamusenda iye, ndipo Sarah anamuwuzwa kuti apange mkate ndi kukonzekera kuti awadyetse iwo.

67 Tsopano kumbukirani, awiri a iwo anali Angelo, Angelo mu mnofu waumunthu, ndipo mmodzi wa iwo anali Mulungu Mwiniwake. Ndipo Mmodzi yemwe anali Mulungu anali nsana wake atautebenezira ku hema.

68 Ndipo Sarah anakhala mu hema. Ine ndimakonda kumuwona mkazi akusunga malo ake monga choncho, osati kumapita panja ndi kumamuwuzwa mwamuna wake choti nkuchita, ndi nthawi iliyonse imene wina akabwera kumeneko. Koma iye anakhala mu hema. Palibe zokaikitsa, mwinamwake akutsuka mbale kapena akuchita chinachake.

69 Ndipo Mmodzi uyu Amene anali Mulungu, Iye anapitirira kuyang'ana mozungulira cha ku Sodomu, ndipo Iye anawauza iwo chimene Iye amati akachite. Ndipo Angelo awiri anapita kumusi mkati mmenemo kuti akalalikire Uthenga. Koma mmodzi anatsalira mmbuyo, ameneyo anali Mmodzi yemwe anali Mulungu, ndipo Iye anati, “Ine sindichita kuzibisa kwa Abrahamu zinsinsi zimene ine ndikuzidziwa, chifukwa iye akhala wolowa wa dzikoli.”

70 O, ife tiri nawo ufulu mmawa uno, mpingo, kuti tidziwe zinsinsi za Kudza kwa Ambuye. Pakuti, “Odala ali opanga mtendere, iwo adzatchedwa ana a Mulungu. Odala ali iwo akuchita njala ndi ludzu, iwo adzakhala ali odzazidwa. Odala ali angwiro mu mtima, pakuti iwo adzamuwona Mulungu. Odala ali ofatsa, pakuti iwo adzalandira dziko lapansi.” Ndiye, ngati mpingo wa Mulungu wamoyo uli woti udzalandire dziko lapansi, palibe zinsinsi zabisidwa kwa iwo.

71 “Zonse zimene Atate andiuzwa Ine, Ine ndakuuzani inu,” anatero Yesu. Ndipo iwo sankakhoza kumukhulupirira Iye.

72 Kotero mu masiku a Abrahamu, monga Iye anali kulozera kwa iwo, Iye ananena kuti monga Abrahamu anali kuyankhula kwa Mngelo, ndipo nsana wake unatembeneziridwira ku hema, ndipo Iye anamuuzwa Abrahamu Iye amati adzamuchezere iye ndi mwana. Ndipo Sarah, mu hema, anaseka. Ndipo Iye anati, “Nchifukwa chiyani Sarah anaseka?” Kodi Iye anali kusonyeza chiyani? “Nchifukwa chiyani Sarah anaseka?” Awo anali maora kuchepa okha chisanachitike chiwonongeko, pamene izo zinali kuchitika. Basi chiwonongeko chisanachitike, moto umenewo unabwera kuchokera kumiyamba ndipo unawutenthapo mzindawo, ndipo chizindikiro chimenecho chinachitidwa.

73 Ndipo Yesu anati, “Inu mukuchita cholakwika,” kwa madokotala aakulu azaumulungu, kwa fuko lachipembedzo kumene kwenikweni mamilioni anali okhulupirira. Iye anati, “Inu mukuchita cholakwika, posadziwa Lemba ngakhale Mphamvu ya Mulungu.” Kwa m'badwo wonga umenewo, amene anali amuna ophunzitsidwa bwino, amene anali masikolala ndi oleredwa ndi mpingo. Pamene mwana anali kubadwa, iye anali chuma cha mpingo. Iwe umayenera kuti ukhale

Muisraeli. Masiku asanu ndi atatu akapita utabadwa, iwo unali mdulidwe, ndipo iwe unali Muisraeri kuyamba ndi kuyamba. Ndipo unsembe unkabwera kuchokera kwa Alevi, amene anali ophunzitsidwa kupyolera mazana a zaka mu Malemba. Komabe Yesu anati, “Inu mukuchita cholakwika, pokhala osadziwa Malemba!” Iwo ankawadziwa iwo mwa mabuku awo omwe ophunzirira, iwo ankawadziwa iwo mwa makatekizimu awo, iwo ankawadziwa iwo mwa zamulungu zawo zawo. Koma Yesu anati, “Inu simukuwadziwa Iwo, Malembawo, inu simukuidziwanso ngakhale Mphamvu ya Mulungu. Ngati inu mukanakhala mutamudziwa Abrahamu, inu mukanandidziwa Ine. Ngati inu mukanakhala ana a Abrahamu, inu mukanandidziwa Ine, chifukwa Abrahamu anakondwera pamene iye anawona tsiku Langa, pakuti iye analiwoneratu tsikulo. Pamene ine ndinayima pamaso pa iye mmbuyo uko, mu thupi la mnofu, ndi kuchita izi, iye anadziwa uyo anali Ine, ndipo iye ananditcha Ine ‘Elohim.’ Koma pano Ine ndikuchita chinthu chomwecho pamaso pa inu, ndipo inu mukunditcha Ine ‘Belezebule.’”

“O,” iwo amakhoza kunena, “ife tiri naye Abrahamu kwa atate athu.”

“Mukumutcha Abrahamu ‘atate’ wanu?”

⁷⁴ Iye anati, “Bwanji, ife, ife ndife a mpingo. Ife ndife fuko la chipembedzo. Ife ndife anthu aakulu. Ife ndife anthu a Mulungu!”

Yesu anati, “Inu ndinu Mdierekezi, iye ndi atate wanu.”

⁷⁵ Kodi ine ndikanawufanizira m’badwo umenewo kwa umodzi uno. Lero, pamene pali kwenikweni mamilioni a anthu amene amadzinenera Chikhristu, ndipo nkusamadziwa mochuluka za Mulungu kuposa momwe Nkafula akanadziwira za walupanga wa Chiigupto. Alipo amuna ndi akazi lero, kwenikweni mamilioni a kudzinenera Chikhristu omwe amadzitengera Khristu, samadziwa mfundo yoyamba ya Mphamvu ya chiwukitsiro Chake, ndipo sanayambe alawapo ubwino Wake. Iwo sanayambe amvererapo Mphamvu Yake. Maso awo achititsidwa khungu kwa Choonadi.

⁷⁶ Anati, “Inu ndinu akhungu, atsogoleri a akhungu. Kodi . . . n . . . ngati wakhungu atsogolera wakhungu, kodi iwo onse sagwera mu dzenje?”

⁷⁷ Ndiye iwo anaganiza, “Ife ndife Akhristu. Ife ndife okhulupirira. Ife ndife a mipingo yapamwamba imene ilipo. Aphunzitsi athu ndi masikolala ophunzitsidwa bwino kwambiri amene alipo.” Ndipo komabe Yesu anawauza iwo kuti iwo sankadziwa ngakhale Malemba.

⁷⁸ Mukuona momwe Mulungu anabisira izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndi kuziulula izo kwa makanda monga amene ati adzaphunzire? O, mphamvu yaikulu ndi kupanda malire kwa Mulungu! Momwe Iye aliri wabwino kwa omwe akukhumba

kuti aziyenda molunga pamaso pa Iye! Iye sadzawabisira kanthu kabwino kalikonse.

⁷⁹ Ndipo kuwona tsiku limene pamene fuko lathu, dziko lathu, lavunditsidwa ndi chinthu chomwecho!

⁸⁰ Yesu ankafuna kuwawongola iwo moyenera. Iwo anati, “O, Abrahamu ndiye atate athu. Ndipo ife tidzakhala mu Ulemerero, musati inu mudandaule za zimenezo, chifukwa ife timakhulupirira mwa Mulungu. Ife ndife aphunzitsi, ndipo ife timakhulupirira mwa Mulungu, ndipo ife timawaphunzitsa anthu athu. Ndipo Iwe ndiwe yani kuti ubwere pozungulira pano ndi—kachizindikiro kakang’ono kachinsinsi kachikale ndi kuyesa kuzitcha izo Mulungu? Iwe siuli kanthu koma Belezebule.” Apo inu muli, iwo anali nato tizikhulupiro tawo ndi chipembedzo chawo.

Yesu anawauza iwo, “Ndinu Mdierekezi.” Taganizani za izo!

⁸¹ Ndipo ine ndikanawufanizira m’badwo umenewo kwa uwu, lero pamene ife tiri nawo mamilioni olowa mipingo, ife tiri nawo makumi a zikwi. Ndipo Mulungu amabwera pansu kuti adzakhale mu mpingo Wake kachiwiri, ndi kuti adzachite zinthu zomwezo zimene Iye anachita kumeneko, kuti adzipange Iyemwini yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Ndipo anthu akutembenezira nsana wawo kuchoka kwa izo, mowirikiza, ena kuti akhale otchuka, ena kuzemba kuti apange kusankha. Izo zakakamizidwira pa anthu! Iwe uyenera kupanga kusankha. Iwe sungakhoze kuyima pakatikati. Iwe uyenera kunena “inde” kapena “ayi.” Iwe sudzachoka konse pa khomo ilo munthu yemweyo amene iwe unabwera mkati. Iwe sungakhoze kuchita izo. Iwe uli nako kusankha koti upange. Kupangireni iko kwa Khristu mmawa uno.

⁸² Iwo ankaganiza chirichonse chimene chinali cha mpingo chikanati chidzapulumutsidwe. Yesu anati, “Khwala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

⁸³ Ndiroleni ine ndikuchenjezeni inu mmawa uno, mpingo, khalani osamalitsa. Izo zimatenga nthawi lero, mu chirungamochawekha chathu, kukhutitsidwa-kwawekha, m’badwo wa chinyengo umene ife tiri kukhalamowu. Ora limene pamene amuna ndi akazi amayima mu mipingo ndi mu mipando, ndi kumayimba nyimbo za Mulungu, ndi kuyenda akutuluka mu tchalitchi chimenecho ndi kukasuta ndudu, ndi kukamwa kachasu, ndi kupita kuzovina, ndi—ndi kukhalira moyo kwa dziko, ndi kunena nthabwala zauve, zakuda, ndi kudzitcha okha “Akhristu.” Pamene amuna ndi akazi angakhoze kuyenda kuchokera pa guwa kapena kuchokera ku mpingo, ndi kuchokera ku malo a Mphamvu ya chiwukitsiro, pamene chizindikiro chomwe chija cha Umesiya chikusuntha pakati pawo, ndipo nkusakhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu,

apo pali chinachake cholakwika. Pamene mapepala angakhoze kuzifalitsa zimenezo; ndipo kuchokera ku gombe kupita ku gombe, mmbuyo ndi mtsogolo, kuchokera ku zigawo zachisanu za Kumpoto kupita ku nkhalango zotentha za Kummwera, Mulungu akutumiza izo, ndipo anthu mowirikiza akutembenezira nsana wawo pa Izo. Ndiye ife tingakhoze kunena chiyani, ife tingakhoze kuchita chiyani? Ife tibwerera mmbuyo ku Malemba kumene Iye anati, “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

⁸⁴ Iye anati, “Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa, chotero izo zidzakhalanso mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Mvetserani, mu masiku a Nowa, dziko linadzazidwa pafupifupi monga ilo lirili lero. Sayansi yawo inali yoposa yathuyi. Iwo ankamanga masinfikisi ndi mapiramidi ndipo anachita zinthu zimene ife sitingakhoze kuzichita lero. Zoposa, zazikulu, anthu aluntha. Ndipo kumbukirani, sayansi imanena lero, “Ili miniti imodzi usanafike pakati pa usiku.” Ili miniti imodzi kuti koloko igunde ora la kufa. Ndi mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira. Ine ndikuyembekeza kuti—ndikudalira kuti Mzimu Woyera umiza izi kupita mu mtima wa wokhulipirira aliyense, “monga masiku a Nowa”!

⁸⁵ Ndi angati amene anapulumsidwa mu masiku a Nowa, kuchokera mu m’badwo umenewo? Asanu ndi atatu, asanu ndi atatu kuchokera mu mamiloni ambiri. Iye anati, “Kotero izo zidzakhalala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu.”

⁸⁶ “Ndipo monga izo zinali mu masiku a Sodomu, kotero izo zidzakhalala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Pa opitirira makumi a zikwi, uko kunali atatu amene anapulumsidwa.

⁸⁷ Inu munganene kwa ine ndiye, “Mlaliki, bwanji zikwi zonse zimene ziti zizikabwera ndi Iye?” Tsopano, m’bale, zimenezo zinapangidwa kupyola mu mibadwo yambiri.

⁸⁸ Ine ndidzakhalala wodabwitsidwa ngati dazeni iti ituluke kuchokera mu m’badwo uno. “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

⁸⁹ O, ine ndikudziwa mipingo, chimene iyo imanena, “Ngati iwe uyika dzina lako pa bukhu ndipo iwe kukakhala membala, *uwu*, iwe uli bwino.” Palibe Lemba loterolo monga zimenezo. Ngati chirichonse chiri nalo dzina lake pa bukhu, ndi mu—mu mpingo, apo adzakhalapo bilioni kuchulukitsa ndi bilioni kuchulukitsa ndi bilioni, chirichonse chidzakalowa mkati. Ndiye mitundu yonse ya mizimu idzakakhala mkati mmenemo, ndipo ndi chikhalidwe cha mtundu wanji chimene Kumwamba kuti kudzakhalale ndiye? Taganizani za zimenezo tsopano.

⁹⁰ Winawake akanati anene kwa ine, “Tsopano dikirani miniti, M’bale Branham. *Akuti-ndi-akuti*, ine ndinawamva iwo akuyankhula mu malirime, ine ndikudziwa iwo akafika uko.”

⁹¹ Izo sizikutanthauza kuti iwo akafika uko konse. Paulo anati, mu 1 Akorinto 13, “Ngakhale ine ndayankhula ndi lirime la anthu ndi angelo, ndipo nkusakhala nacho chikondi, ine sindiri kanthu.”

⁹² “O, ine ndinapita ku msonkhano wa *Akuti-ndi-akuti*. O, iye anachita ntchito zazikulu, zamphamvu. Ine ndinamuwona iye akuwapanga akhungu kuti apenye.”

⁹³ Komabe iye akanakhoza kukhala wotayika. “Ambiri adzadza kwa Ine mu tsiku limenelo ndi kunena, ‘Ambuye, kodi ine sindinalalikire ayi mu Dzina Lanu, kunenera? Kodi simunali, mu Dzina Lanu, ine ndinkatulutsa mizimu yoyipa? Kodi simunali, mu Dzina Lanu, ine ndinachita ntchito zambiri zazikulu?’ Iye adzanena, ‘Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaweruzika, Ine sindinakudziweni inu nkomwe.’” “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

⁹⁴ Ndiroleni ine ndikupatseni inu kufanizitsa kwina kumene kuti kukugwedezeni inu. Malingana ndi sayansi ya zamankhwalala, mu mzinda wa Chicago, malingana ndi kuwerengera kwa madokotala, kuti muli mirandu ya kutaya mimba zikwi makumi atatu mu Chicago mokha, mu masiku makumi atatu, imene madokotala ali nayo. Ndi ingati ya mapilisi aang’ono awa ndi zinthu zimene iwo amamwa, za milandu ya kutaya mimba?

⁹⁵ Chiwerengero chikusonyeza, mu United States, kuti alipo ana ochulukirapo apathengo amene amabadwa kuposa amene ali ana a mchikwati choyera. Kodi inu mumadziwa kuti Baibulo linanena, mu Deteronome 14:2, kuti “mwana wapathengo, izo zikanatenga zaka mazana anai kuti izo zitheretu”? Ana a ana awo ana a ana awo a ana awo sakanakhoza kukayima mu msonkhano wa Ambuye, zaka mazana anai, mibadwo khumi. Zaka makumi anai mu m’badwo. Agogo-agogo-agogo-a agogo-agogo-a agogo-a agogo awo amuna anali mwana wapathengo, iye wachokapo pa chithunzicho! Tsopano chiyani? Ndisonyezeni ine pamene izo zinasinthidwira.

⁹⁶ Kodi ife tikubwera ku chiyani? Ndipo tsopano apathengo, chifukwa cha chigololo, ndipo akazi odzaza machimo akuvala pa misewu monga amuna, chimene chiri themberero pamaso pa Mulungu, osuta ndudu, akumwa paphwando, otchedwa Akhristu odzinenera. Mulungu amaletsa gulu loterolo la aziwerewere! Ndiko kulondola. Ndiye nkumadzitcha iwo okha Akhristu? Palibe zodabwitsa kuti Yesu anati, “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, koma apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

⁹⁷ Iwo sangakhoze kudzichepetsa okha. Iwo ali okhuthara. Onani, pamene Davide anauzidwa za tchimo lake limene iye analichita, mwamsanga iye analapa, ndipo Mulungu anamukonda iye chifukwa cha chimenecho. Iwe ukawauza iwo za machimo awo, iwo ati, “Ine sindidzachtitsanso mdima chitseko icho kachiwiri.” Chifukwa chiyani? Iwo ali nawo malo ochuluka kuti apiteko, iwo akhoza kupita ku mphanga za apathengo awo amene angalolere zoterozo. Koma ndi nthawi yoti alaliki avale zida mwathunthu za Mulungu ndi kulalikira Mawu mopanda kunyengerera, Uthenga. Anthu ayenera kudzichepetsa okha.

⁹⁸ Palibe kudzipereka pakati pa Akhristu panonso. Iwo akufuna aziti, “Ine ndine wa Methodisti, ine ndine wa Baptisti, ine ndine wa Chipentekoste,” zimenezo sizimatanthauza [M’bale Branham akhwatchitsa chala chake—Mkonzi.] *choncho* kwa Mulungu.

⁹⁹ “Ine ndinayankhula ndi malirime, ine ndinachita zozizwitsa.” Ife timayika kutsimikizira konse pa zimenezo, pamene ndicho chimodzi cha zinthu zochititsa khungu kwambiri zimene iwo angakhoze kuchita. Zedi. Mvula imagwera pa olungama mofanana basi ndi pa osalungama. Mvula imatsirira mbewu mofanana monga iyo imatsiririra maudzu, Roy. Mvula yomweyo, Mzimu Woyera womwewo umagwera pa anthu. Izo apobe sizimatanthauza... Chikhalidwe chawo chiyenera kuti chikhale chosiyana, kuchokera mkati mpaka kunja. Osati kuwonetsera kwa kunja kapena chiwonetsero, koma Mzimu wamkati wa Mulungu wamoyo womwe umamupanga munthu ameneyo cholonedwa chatsopano, womwe umachepetsa mtima wa mwamuna kapena mtima wa mkazi pamaso pa Mulungu.

¹⁰⁰ Inu mukuti, “Mlaliki, inu mukufuna kutanthauza kuti mundiuze ine kuti inu mukukayikira dazeni kuchokera mu mamilioni awa ndi anthu mabilioni anai mu dziko?” Ine ndikukayika ngati ati adzakhalepo dazeni amene ati adzakwanitse Mkwatulo. Taganizani za zimenezo! Ine ndikukuuzani inu zimene Yesu ananena pano mu Uthenga. Taganizani za zimenezo!

¹⁰¹ Kodi izo zafika ku chiyani? Chifukwa makhalidwe oyipa anafika pakati pa anthu, ana apathengo anayamba kukhala akubadwa, amene zinawafutapo iwo. Onani, ife tikhoza kuyima pano kwa maora, kuyika pamalo zinthu zimenezo, ndipo inu mukhoza kuwona kuti ife tikukhala mu m’badwo wovunditsidwa, wotemberereka, wovunda-mpaka-pachimake wa anthu. Palibe zodabwitsa kuti iwo palibe zizindikiro angakhoze kuziwona, palibe zodabwitsa iwo sakhoza kumvera Uthenga, iwo awumitsidwa, komabe kungokhala achipembedzo ndi odzichepetsa mwabodza.

¹⁰² Kodi Yesu sananene kuti, “Mzimu ukuyankhula momveka, mu masiku otsiriza iwo adzakhala ammutu, odzikuza, okonda zosangalatsa koposa za Mulungu, okana choonadi, amwano, olusa, ndi onyoza iwo amene ali abwino, okhala nawo mawonekedwe aumulungu”? Mwaona? O, iwe ukhoza kufuula, zedi. Iwe ukhoza kuyankhula ndi malirime, zedi. Chikhulupiriro chidzathamangitsira kunjwa ziwanda, zedi. Koma izo siziri zimene ife tikuzikamba.

¹⁰³ Ndiye inu mukananena kwa ine, “M’bale Branham, chilemba cha Chikhristu ndi chiyani? Ndi ndani yemwe ati adzapulumutsidwe? Kodi ndinu, M’bale Branham?” Ine ndikudalira zimenezo kwa Mulungu. Ine sindikudziwa. Ine ndikukhulupirira kuti ine ndiri. Ine ndikufanizitsa moyo wanga, tsiku ndi tsiku, ndi Mawu. Ngati iwo siukhala mpaka pa Mawu awa, ndiye pali chinachake chalakwika, ine ndiyenera kuti ndibwerere mmbuyo ndi kukakhala bwino.

¹⁰⁴ “Chabwino,” kuti, “M’bale Branham, pamene anthu ayankhula ndi malirime, kodi izo sizimatanthauza kuti iwo ali opulumutsidwa?” Ayi, bwana! Ayi, indedi! Ine ndamvapo mfiti zachimuna ndi zachikazi zikuyankhula ndi malirime. Mitundu yonse ya zamkutu. Ine ndawaonapo anthu akuyankhula ndi malirime ndi kumakhala ndi mkazi wa mwamuna wina. Ine ndawaonapo anthu akuyankhula ndi malirime, ndi kumadumphira mmwamba-ndi-pansi ndi kumafuula ngati nyumba inali pa moto, ndi kutuluka kunjwa ndi kumakapanga akatangale okhotakhota, ndi kuba, kunena mabodza, ndi chirichonse. Inu mungakhoze bwanji kuyembekezera zimenezo? Ayi, bwana.

¹⁰⁵ Kukhala mu mpingo, madikoni mu mpingo, odzichepetsa mwabodza monga iwo angakhoze kukhalira. Chifukwa chiyani, inu mukuganiza kuti iwo amagula petulo Lamlungu? Ayi. Koma Lolembe kuchita chinachake chimene chiri chauve ndi chovunda ndi chotsikira-pansi. Mulungu amakhala mu mtima, osati kunjaku, ndi chinachake chimabwera kuchokera mu mtima.

¹⁰⁶ “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhala amene ati adzayipeze iyo.” Monga izo zinaliri mu masiku a Nowa, asanu ndi atatu kuchokera mu mamiloni amenewo; monga izo zinaliri mu masiku a Sodomu, atatu kuchokera mwa mamiloni; kotero izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu.

¹⁰⁷ Ndipo inu mukuona chivundi chimene ife tirimo. Inu mukuona momwe lingaliro lirilonse, munthu, iye amafika kunjwa uko ndipo Mdierekezi amapanga alaliki ophunzira kumayima mu guwa ndi kuwalola anthu kumapitirira nazo zimenezo.

¹⁰⁸ Tsiku lina munthu anati, “Ine sindikanalola iwe kuti ukhale mu guwa langa, iwe ukanawapangitsa azimayi anga kuchita misala.” Ayi, iwo ali kale mwa njira imeneyo. Izo

zikanawabweretsa iwo ku malingaliro awo abwino, kuwauza iwo pamenepo kuti asiye kuvala zovala izi ndi zinthu. Ndipo, chabwino, winawake ayenera kuti achite izo.

¹⁰⁹ Ine ndinanena kwa mkazi wanga, “Kodi ine ndikuyamba kupenga, mwiniwanga? Kodi ndine wamisala? Kapena chavuta ndi chiyani ndi ine?” Chinachake mkati umu sichingakhoze kugwira chete. Ine ndiyenera kuti ndichinene Icho, ine sindikusamala chimene aliyense akunena.

¹¹⁰ Mukuti, “Iwe uwononga utumiki wako.” Chabwino, utumiki uliwonse umene Uthenga ungawuwononge, uyenera kuti uwonongedwe. Mulungu tipatseni ife kulimbamtima kuti tiyime ndi chimene chiri Choonadi ndi kunena Choonadi za icho! Ndi tchimo, zamanyazi!

¹¹¹ “Khwalala ndiro chipata,” anatero Yesu, “ndipo njirayo ndi yopapatiza.” Ndipo inu amene mukuganiza mamilioni, ndi nonse inu Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achipentekoste mukukalowa mkati, inu mudzapusitsidwa pa tsikulo. Yesu anati, “Ambiri adzadza ndi kukhala pansu mu Ufumu, kunena, ‘ine ndiri nawo ufulu kuti ndikhale muno.’” Iye anati, “Koma ana a Ufumu adzawatulutsira iwo kunja. Kumeneko kudzakhala kuli kulira ndi kubuma ndi kukukuta kwa mano.” Kulibwino utenge kufufuza mmawa uno, Mkhristu. Kumeneko kudzakhala kuli khumi kuchulukitsa mamilioni kuchulukitsa mabilioni a Akhristu odzinenera, ndi olimbika mu moyo wawo, amene ati adzachiphonye chipatacho. Yesu ananena choncho.

“Ndi angati amene ati akalowe mkati?”

¹¹² Ine sindikudziwa ndi angati ali kupita. Chinthu chokha ndicho, “Mulungu, mudirole ine ndikhale mmodzi wa iwo!” Ndi chimenecho. Iye ndiye Woweruza. “Ndiroleni ine ndikhale mmodzi.”

¹¹³ Inu mukuti, “M’bale Branham, inu mungakhoze kumudziwa bwanji ndiye pamene ali Mkhristu?”

¹¹⁴ Ine sindikudziwa. Koma ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chimene Lemba limanena. Zedi inu mukhulupirira Izo. Pamene Mzimu Woyera unatumizidwa ku dziko lapansi, Mulungu anayankhula kupyolera mu Mzimu Woyera. Iye anatomiza mngelo, choyamba, kumeneko choyamba, ndipo Iye anati, “Pita kupyola mu mzinda ndi pakati pa anthu, ndipo kayike chilemba pa mphumi pawo, cha iwo amene akuwusamoyo ndi kulira chifukwa cha matemberero, kukonza zinthu zimenezo.”

¹¹⁵ Themberero ndi chiyani? Mkazi yemwe angavale chovala chimene chiri choyenera kwa mwamuna. Izo zimamupangitsa Mulungu kudwala. Kodi inu munayamba mwapita pozungulira pamene chinachake chiri chotembereredwa? Momwe icho kudwalitsa komwe chimakupangitsa iwe! Iwe sungakhoze kupirira icho. Mkazi yemwe angavale chovala chimene chiri choyenera kwa mwamuna, umo ndi momwe zimampangitsira

Mulungu kumverera; iwe ukhoza kumayimba mu kwayara, iwe ukhoza kumapemphera tsiku lirilonse, ndi kumafuula tsiku lirilonse, kapena kukhalira moyo Mulungu tsiku lirilonse, ndiwe wotsutsidwa mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndi chimodzimidzi zimene Lemba limanena. “Themberero!” Ndipo iwo amene amathandizira zoterozo adzakhala nalo gawo ndi oterowo.

¹¹⁶ Mulungu tipatseni ife chisomo kuti tiyime motsutsa zoterozo. Ngati iwe usowa kuti uyime mwa wekha, ima pamenepo ndi kugwira Mawu a Mulungu mu dzanja lako. Iwo sadzalephera konse.

¹¹⁷ Tsopano ife tafika ku tsiku limene themberero la anthu. Ndipo Angelo apita chotero akusindikiza kachiwiri. Ndipezereni ine munthu mmodzi mu Jeffersonville, ngati inu mukufuna kuti mudziwe yemwe ati akafike uko, ndipezereni ine munthu mmodzi mu mzinda wathu yemwe amausamoyo ndi kumalira, kusautsidwa mowirikiza ndi kutopetsedwa, ndi kumapemphera zotembereredwa zimene zikuchitidwa mu mzinda. Kodi inu mungakhoze kukweza dzanja lanu ndi kuliyika ilo pa munthu mmodzi? Ndiye tengani Lemba ili, “Khwala ndiro chipata, ndipo njira ndi yopapatiza, imene ikutsogolera ku Moyo, apang’ono kumeneko adzakhala amene ati adzayipeze iyo.” Ndiwo amodzi okhawa amene anali oti asindikizidwe.

¹¹⁸ O, ine ndikhoza kukusonyezani inu ochuluka opita ku tchalitchi. Ine ndikhoza kukusonyezani inu ochuluka oyimba mu kwayara. Ine ndikhoza kukusonyezani inu ochuluka ophunzitsa Sande sukulu. Ine ndikhoza kukusonyezani inu ochuluka omwe ali mkulu wa—wa magulu aakulu. Ine ndikhoza kukusonyezani inu ochuluka amene amafuula, ochuluka amene amayankhula ndi malirime, ochuluka amene amagwira ntchito mu ntchito ya Uthenga.

¹¹⁹ Koma ndisonyezeni ine mmodzi yemwe pansu mu mtima wawo akuvutitsidwa kwambiri pa machimo a dziko! Ndisonyezeni ine mlaliki amene angakhoze kuyima lero ndi kutsutsa zipembedzo zimenezo. Ndisonyezeni ine mlaliki yemwe ati adzayime ndi kunena zinthuzo, ndi kutsutsa zipembedzo zimenezo. Iye kulibwino asatero, iye adzakankhidwira kunjira, icho ndi chiphaso cha zakudya.

¹²⁰ Nzosadabwitsa Bill Graham anamuza Jack Moore, anati, sakuwona momwe misonkhano yanga ikuyimira, anati, “Iye sali wa Baptisti, ngakhale kuti ali iye wa Methodist kapena Pentekoste.” Anati, “Ndipo onse a iwo akumutsutsa iye.” Zedi, ine sindikunena izo... Chifukwa chimene ine ndinati, ine sindingakhoze kuzinena izo mu chigulu. Ine ndikunena izo kwa mpingo wanga womwe. Ine ndikukhala nako kulimbana, chifukwa ora loyesa liri pa ine.

121 Iwo amati, “Ngati iwe uti ubwere, izo zikhala zabwino, koma iwe usati unene kanthu zokhudza Izo.” Iwe basi mwina ukanangoti usunge mpweya wako.

122 Ine ndizilalikirira chimene Mulungu anati lalikirira! Ndiko kulondola. Mmodzi wa asanu ndi atatu awo adzakhala penapake. Mmodzi wa iwo adzakhala penapake. Koma pa tsiku limenelo ine sindikufuna kuti ndidzakhale wolakwa pa kunena kuti ine ndinanyengerera chifukwa cha chikhulupiriro china kapena chiphunzitsa china cha mpingo, kapena chipembedzo china. Ine ndalalikirira Choonadi!

123 Iwo amati, “Bwanji inu, bwanji usali utumiki wanu, M’bale Branham, umene umawoneka kuti uli wawukulu chotero, chifukwa chiyani iwo sukusesa kunja monga amuna ena awa akuchitira?”

124 Ndi zimenezo apo pomwe. Ndi zimenezo. Ine ndikapita mu mzinda, kodi inu mukuganiza kuti a Assemblies of God angagwirizane nane ine? Osati pa zimene ine ndimakhulupirira, iwo satero. Ndikhoza kupeza mmodzi kamodzi pa nthawi. Inu mukuganiza kuti Amethodisti akanatero? Yesani, ndipo fufuzani. Mukhale manenjala wanga kwa sabata. Ngati inu mukalowa umo, inu mukalowa umo mu Dzina la Yesu. Ndiko kulondola.

125 O, zoonadi, iwo amakutengera iwe kumeneko, zedi, kukutengera iwe kumeneko penapake mu malo, ndipo kotero kuti iwe usalumikizane ndi iwo mu njira zirizonse monga choncho. Ndiyeno pamene iwe uchoka, amati, “O, tsopano, M’bale Branham wakhala ngati wosokonezeka mu ubongo pang’ono pokha basi, inu mukudziwa. Iye . . .”

126 Ngati ine ndiri wosokonezeka mu ubongo, ndiye Baibulo laphonya mu Kuphunzitsa. Ndizo zimene Baibulo linanena! Inde, bwana. Penyani!

127 Yesu anati, “Nchifukwa chiyani inu mukunditcha Ine ‘Bezezebule’? Inu munamukhulupirira Solomoni, chizindikiro chake cha kuzindikira za mu mtima. Inu munakhulupirira tsiku lake. Mfumukazi ya Kummwera inabwera kuchokera kumapeto kwenikweni a dziko lapansi, kuti idzawone mphatso imeneyo, ndipo iye anayikhulupirira iyo pamene iye anayiwona iyo. Ndipo inu mumakhala ndi kumayang’ana pa iyo tsiku ndi tsiku, ndipo simuyikhulupirira iyo.”

128 Ndipo abale Ake Omwe sanamukhulupirire Iye. Anati, “Iwe pita ku phwando uko,” Iye anati, “koma Ine sindipita uko tsopano.” Iye anapita uko njira yina, chifukwa abale Ake Omwe sanali kumukhulupirira Iye. Ndiko kulondola. “Khwala ndiro chipata, ndipo njira ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhhalapo amene ati adzayiyeze Iyo.”

129 Pamene izo zinafika kwa ophunzira, ku chiwonetsero, kodi iwo anali ali kuti? Mkazi ndi mwamuna anayima pafupi ndi mtanda ndi Iye, Yohane ndi Maria. Onse a iwo anali atapita.

130 Ichi ndi chiwonetsero. Iyi ndiyo nthawiyo. Apa ndi pamene Mulungu akuchita zinthu. Apa ndi pamene Mesiya ali pa dziko lapansi. Apa ndi pamene Mphamvu ya Mulungu ili kusunthira mwa anthu Ake. Ndipo iwo akuwatchesa iwo “oyera-odzigudubuzwa, openga, amisala,” o, zonga zimenezo. Koma ora liri pano!

131 Uko ndithudi kukakhala zokhumudwitsa zina zazikulu pa chiweruzo.

132 O, wogulitsamowa, iye amadziwa kumene iye ati adzakakhale pa chiweruzo. Chomwecho ndi momwe garuwamowa amadziwira kumene iye ati adzakayime. Chomwecho ndi momwe wachiwerewere amadziwa kumene iye ati adzayime. Chomwecho ndi momwe wanjuga amadziwira kumene iye ati adzakayime. Chomwecho ndi momwe chidakhwa chimadziwira kumene iye ati adzayime. Iye sadzakhumudwitsidwa ayi.

133 Koma kumene kukhumudwa kuti kudzakhala, ndi iwo amene ankaganiza kuti iwo anali akulondola. Ndipo pali kukhumudwa. “Pamene iwo adzafika kumwamba uko, adzati, ‘Zedi, ife tinatulutsa adierekezi mu Dzina Lanu. Ndife alaliki. Ife ndife a mipingo yakuti-yakuti. Ife tinachita zozizwitsa zazikulu. O, ife tinalalikira! Bwanji, ine ndakhala ndiri—ine ndakhala ndiri wosamalira chuma mu mpingo. Ine ndakhala ndiri bishopu. Ine ndakhala ndiri *ichi*.’ Chokani kwa Ine, inu ochita za kusaweruzika, Ine sindinakudziweni inu nkomwe.” Pamenepo inu muli. Ndiko kukhumudwa. Iye anati, “Ana a ana awo adzabwera mkati ndi kukhala pansu mu Ufumu, nkuti, ‘Ifi tiri nawo ufulu woti tikhale muno,’ ndipo iwo adzaponyedwera kunja ku mdima wakunja, kumene iwo azikakhala akulira ndi kubuma ndi kumakukuta mano.” “Khwala ndiro chipata, njira ndi yopapatiza, imene ikutsogolera ku Moyo, apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

134 Kwa inu, anthu okonedwa anga, mmawa uno, mvetserani kwa izi. Ine sindinazipange izi. Ine ndiri wokhudzidwa pa kuzinena Izo. Ndicho chonse chimene ine ndiri ndi udindo nacho. Ngati ine sindilalikira konse ulaliki wina mu moyo wanga, chimenecho ndi Choonadi: uko kukakhala anthu apang’ono okha atapulumutsidwa. Ingokumbukirani zimenezo: apang’ono kwambiri okha. Inu mudzakhale mmodzi wa iwo.

135 “Iwowo ndi wati, M’bale Branham?” Ine sindikudziwa. Palibe winawake ankadziwa. Ife timagwirira ntchito chipulumutso chathu chomwe ndi mantha ndi kunjenjemera.

136 Koma inu mukhale ofola ndi Mulungu. Ngati mtima wanu sulikugunda basi ndi Baibulo limenelo, ndiye pali chinachake

chalakwika, pali chinachake chalakwika. Ziribe kanthu chimene mpingo wanu unena, inu simungakhoze kulowa mkati ndi iwo. Inu muyenera kukalowa mkati ndi zimene Mulungu ananena. Ili ndi Bukhu limene inu muti mudzaweruzidwe kuchokeramo, Baibulo. Khalani ndi Ilo!

137 “O,” inu mukuti, “chabwino, ine ndabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu.” Ndiko kukhoza, ndilo Baibulo. Koma ngati moyo umenewo suli kutsatira ilo, izo sizinakuchitireni inu ubwino wochuluka kuti mukhale obatizidwa.

138 Inu mukuti, “Chabwino, ine ndiwulandira Mzimu Woyera.” Ndizo zabwino, ndicho chimene inu mukayenera kukhala mutachita. Koma ngati moyo mulibemo mkati umo!

139 Kumbukirani, udzu umalandira mphamvu yomweyo imene imagwera pa tirigu kuti ikamupangitse iye kukula, imapangitsa udzu kufuula, nawonso. Udzu wakale wawung’ono umenewo umayima tsonga ndi wokondwa basi monga tirigu ali. Ndiko kulondola, umakhala moyo ndi moyo womwewo. Ndipo wochimwa akhoza kukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu, kufuula chigonjetso, ndi kumakhala monga Mkristu. Koma ngati umo mulibe chinachake chosiyana mu mtima! Iye akhoza kukhala ndi Mphamvu yomweyo kuti azitulutsira kunja mizimu yoyipa. Yesu ananena choncho. Iye akhoza kumalalikira Uthenga mwabwino basi monga mlaliki wina aliyense angakhoze kuchitira. Ndizo chimodzimidzi zimene, Yesu ananena choncho. Baibulo limaphunzitsa zimenezo. Inde, bwana. “Ngakhale ine ndiyankhula ndi lirime la anthu ndi angelo, ngakhale ine ndipereka thupi langa kuti liwotchedwe ngati nsembe, ine ndipereka katundu wanga yense kuti ndidyetse osauka. Ine—ine ndiri nacho chikhulupiriro choti nkusuntha mapiri, ine ndikumachita zinthu zonse izi, ine ndikamalalikira mu Dzina Lake, ine ndikamatulutsa adierekezi mu Dzina Lake,” iye anati, “ine sindine kanthu.” Kotero, iye akanakhoza kumachita izo, ndipo “sikanthu.” Mwaligwira lingalirolo?

140 Tsopano, chinthu choti nkuchita, kuchokera mu mtima wanu, khalani Mkristu, tsopano lowani mkati pa chipata cha khwalala. Pakuti, njira ndi yotakata imene ikutsogolera ku chiwonongeko, ndipo mamiloni kuchulukitsa ndi mamiloni mu m’badwo uno wa okhulupirira adzalowa kudzera pamenepo. Chifukwa, khwalala ndiro chipata, ndipo njira ndi yopapatiza, iwe ndi Khristu nokha.

141 “Njira ndi yopapatiza imene ikutsogolera ku Moyo, ndipo apang’ono okha kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.” Tsopano, ndiwo Mawu a Ambuye wathu. Mai! Kodi Iye anali kuchita chiyani? Kuyima pamenepo, kuzindikira malingaliro awo.

142 Ndipo iye anati, “Iye ndi Bezezebule. Chabwino, Iye angakhoze bwanji kukhala Mulungu? Iye ndi Munthu! Kodi nzeru iyi inkachokera kuti?” iwo anatero mu mzinda Wake Womwe.

143 Pamene iwe uyenda kupita mu mzinda kuno, izo zimawoneka ngati. . . Ine sindikunena izi mosalabadira konse kwa inu anthu; ndinu Mkhristu, inu mumandikonda ine. Iwe ukayenda kupita mu mzinda kuno, ndipo izo zimawoneka ngati kuti mphamvu ya Satana ikukugwetsera iwe pansi. Malo awa atsutsidwa. Mzinda uno watsutsidwa.

144 Kodi Billy Graham ananena chiyani pamene iye analowa mu Louisville? Iye anati ndiwo “malo amphamvu ya ziwanda kwambiri” amene iye anayamba wawawonapo mu moyo wake. Anaziyika izo mu pepala, anati, “Iwe ukhoza kungomverera kupsyinja kwa Mdierekezi.”

145 Zoon, ine ndingamverere izo. Chifukwa chiyani? Kuno ndi kwathu komwe. Pamene Yesu anabwerera ku mudzi Kwawo Komwe, Iye anati, “Ntchito zambiri zamphamvu Iye sakanakhoza kuzichita, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo.” Anati, “Mneneri ali wosapatsidwa ulemu, mlaliki, kupatula kukakhala kwawo komwe—mu dziko lake lomwe, pakati pa anthu ake omwe.” Mwaona? Inu simungakhoze kuthandizira izo, Lemba limanena chomwecho. Mukuona?

146 Tsopano, pamene inu muyenda kulowa mu mzinda kuno! Ndipo musati mudiuze ine kuti ine sindikanadziwa. Ine ndimayenda kwa anthu amene amagwedeza dzanja langa ndi kunena, “O, M’bale Branham, ine ndimakukondani inu.” Ndipo iwe nkudziwa kuti ndi bodza! Iwe ukudziwa kuti ndi bodza. Ngati Mulungu angakhoze kundiuza ine kuzindikira za mtima, nchifukwa chiyani Iye sangandiuze ine zimenezo?

147 Zedi, ndipo pakati pomwe pa abale ako omwe ozungulira mzinda! Pamene iwo akuwona iwe, amati, “Chabwino, inu mukudziwa, ine ndinawona pamene wakuti-wakuti. . .”

“Kuti? Zinali kuti izo?”

“Kumtunda uko. . .”

“Ha! Ife tikumudziwa munthu ameneyo!”

148 Iwe umamverera izo. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, inu mumulole winawake kuti abwere mu nyumba yanu yemwe samakukondani inu mochuluka kwambiri, akhale mu nyumba yanu mwa pang’ono pokha ndipo umverere kumverera kwachirendo uko. Chulukitsani izo ndi zikwi khumi ndi zinai tsopano, ndiye inu mupeza chimene ine ndikuchikamba. Ndiye inu mufike mu malo amene aliyense akukukondani inu, kumverera kolandiridwa uko, basi, o, mai, ndipo iwe ukhoza kungokhala pamenepo kwa nthawizonse, onani. Ndi zimenezo,

onani, ndi mzimu. Ndipo anthu samadziwa chimene izo ziri, iwo amadabwa chifukwa chimene anthu ali ovunditsidwa chotero.

¹⁴⁹ Nchiani chimene chimapangitsa akazi abwino, nchiani chimene chimawapangitsa akazi abwino kuvala zovala zachabechabe izo ndi kupita kunja uko? Nchiyani chimapangitsa, ngakhale tsopano pamene kukadali kozizira, asungwana a usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi, atavala zovala zimene iye sakuyenera kuzivala pamaso pa amayi ake, ndipo kunja pa msewu? Ndi chifukwa, osati mwana ameneyo (mwana ameneyo sakudziwa mwa bwinoko mulimonse), koma chifukwa mlaliki wina mu guwa walephera kuti agwire malo ake antchito. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Zedi. Akazi amafika pa msewu, ndipo ovala-mwachigololo monse ndi zinthu monga choncho, ndipo ochimwa amayang'ana pa iwo ndipo samadziwa kuti iye ali wochimwa kumene ngati kuti iye wagona ndi mwamuna ameneyo. Yesu ananena choncho! Yesu anati, "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi ndi kukhumbira pa iye, wachita kale chigololo ndi iye mu mtima wake, ndipo adzayenera kuti ayankhe za icho pa tsiku la chiweruzo." Khwalala ndilo chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza!

¹⁵⁰ Ine ndikudziwa inu mukuganiza ine ndine mnyamata wolimba. Ine sindine wolimba! Ine ndine m'bale wanu, ndipo ine ndimakukondani inu.

¹⁵¹ Thawani mkwiyo umene uli kudza! Pitani ku mtanda ndi kukalira mpaka mtima wanu utadzazidwa ndi Mzimu Wake, chimenecho chidzatembenusa nsana wanu kuchoka ku chirichonse cha mdziko, ndi kuyenda mwaumulungu pamaso pa Iye, ndi mtima wanu ukutenthera kwa Iye. Chikondi! Osati ntchito. Khristu si ntchito, kumutumikira Khristu, ndi chikondi chimene chimamutumikira Khristu. Icho chimakukoka iwe, chimakukakamiza iwe, mpaka kufufuma kulikonse kwa moyo wako kumagunda ndi Iye. Ndi pamene iwe umawona tchimo.

¹⁵² Ndipo Iye analira pa dziko lapansi. Icho chinamukwiyitsa Mulungu mu masiku a Nowa, pamene Iye anawona mitima. Ndipo Yesu anakhala pamwamba pa phiri, ndipo anati, "Yerusalemu, Yerusalemu, ndi kangati kamene ine ndikanati ndifungatire pa iwe, koma ora lako lafika ndipo nyumba yako yasiyidwa yabwinja."

¹⁵³ Kotero izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa Mulungu, mitima ya wokhulupirira wona weniweni yasweka. Iye akuwona pakali pano pakuyenera kukhala chitsitsimutso chikusesa dziko ili. Izo zingakhoze kukhala motani kupyolera mu gulu la apathengo? Izo zingakhoze kukhala motani, pamene iwo ali otsutsidwa kuyamba ndi kuyamba?

¹⁵⁴ Ufumu wa Mulungu uli ngati munthu yemwe anaponyera khoka mu nyanja, ndipo, pamene iye analikokera ilo pa mtunda,

iyeye woti alingalire kuti ziti, iye anangoponyera ilo pa gombe. Ndicho chimene Uthenga umachita. Ndicho chimene Billy Graham, Oral Roberts, inemwini, ndi alaliki ena onse amene akulalikira Uthenga, amawuponya iwo kunjira, ndi kukokera iwo mkati, “Apo iwo ali, Ambuye.” Koma kodi ife tikuchita chiyani nthawi iliyonse? Ife tikupeza kuti, iwe usanati ubwerere kachiwiri, iwo ali mmbuyo mu dziwe kachiwiri. Ndi chiyani chimenecho? Kuyamba ndi kuyamba, uyo anali kamba. Izo sizinamusinthe iye, kuti akodwere mu khoka la Uthenga. Iye anali kamba kuyamba ndi kuyamba. Iye anali nkhasi kuyamba ndi kuyamba. Iye anali njoka kuyamba ndi kuyamba. Iye anali wachinyengo iye asanabwere konse mu mpingo. Iye anali wopanda chikhumbo ngakhale kuti asiye kumwa kwake ndi njuga, ndi kusuta ndi kunama, ndi kuba. Iye anangobwera mkati chifukwa iye anali akuwopa gehena. Iwe ukudzipanga wekha wopitako mochuluka wa iko, pamene iwe ukuchita zimenezo. Ndizo zoonza. “Khwala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.”

Tiyeni tipemphere.

¹⁵⁵ Ambuye, o, ndifufuzeni ine, Ambuye. Weruzani mulandu wanga pakali pano, Ambuye. Musati mudirole ine kuti ndidzachite kubwera pamaso pa chiweruzo pamaso pa Inu, nditatha kulalikira mwa njira iyi. O, ngati pangakhale pali kanthu kalikonse kosayera mwa ine, Ambuye, katengereni iko kutali, chonde! Ife tikuona tsiku limene ife tikukhalamo, pamene amuna ndi akazi akukhala okhuthara kwambiri. Iwo ndi amanyazi. Inu munanena nthawi imodzi, “Palibe ngakhale manyazi pakati pa ana aakazi a Zioni.” Ulemu wawo wachotsedwapo kale chotero mpaka iwo sali ngakhale kuchitanso manyazi. O Ambuye, taganizani za izo! Ndipo kudziwa kuti chowonera nthawi kutsidyako chiri kugunda kutali, miniti chabe kapena awiri ena, ndipo chiwonongeko chachikulu chidzabwera, ndiye msiyeni iye amene ali woyipa akhale ali chiyipirebe.

¹⁵⁶ Mulungu, tidzutseni ife tonse mmawa uno. Tigwedezeni ife, Ambuye! Ife tikuwona zizindikiro zikuwonekera. Ife tapangitsa maso athu kuti atseguke kuti tidziwe zimenezo. Ife tikuwona mamilioni, mamilioni, Ambuye, amene atembenezira nsana wawo ndipo apita kutali. Ine ndikudabwa, chimene ine ndingakhoze kuchita, ine ndingakhoze kuchita chiyani, O Ambuye? Kodi pali chirichonse, Ambuye? Ngati izo zimatengera kulalikira kochuluka, pemphero lochuluka, zochuluka za chirichonse, ndithandizeni ine, Ambuye, kuti ine ndikakhoze kubweretsa Uthenga kwa anthu. Ine ndingakhoze kuchita chiyani? Koma iwo mopitirira akuwutembenezira Iwo pansu. Inu mukuchita zizindikiro Zanu zazikulu ndi kuchita zodabwitsa

Zanu, ndipo komabe anthu akumangoguba kumapitabe patsogolo. Kodi ndi Lemba Lanu kuti liyenera kukwaniritsidwa, kodi ndiyo nthawi imene “Palibe munthu yemwe angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera kwa Ine”? Ambuye Mulungu, perekani mmawa uno kuti anthu awuke ndi kuwona chizindikiro chotsiriza ichi cha dziko lapansi. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mupereke chinachake kwa anthu.

¹⁵⁷ Dalitsani anthu apang’ono awa pano mmawa uno. Mulungu, yambirani ndi M’bale Neville, Ambuye. Chizani thupi lake. Iye ali wodwala mmawa uno, Ambuye, kusokonezeka kwa mmimba. Ine ndikupemphera kuti dzanja Lanu lochiza likhale liri pa iye. Kondwezani moyo wake.

¹⁵⁸ Mulungu, pitani kunja pakati pa osonkhana awa. Alipo amuna ndi akazi amene akhala pano amene ine mwina sindingawawonenso iwo kachiwiri mpaka tsiku limenelo pa chiweruzo, ndiye ine ndidzayenera kupereka umboni. Koma ine ndawerenga Mawu Anu, “Khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhalapo amene ati adzayipeze iyo.” O Ambuye, lolani awa akhale “apang’ono,” amenewo ena a iwo, mutero Inu, Ambuye? Perekani izo munthu aliyense pano.

¹⁵⁹ Ine ndikupemphera monga munthu angakhoze kupempherera mokha. Ambuye, anthu awa akanakhoza kundichitira chirichonse ine, kukamba za kundithandiza ine. Ngati ine ndikanakhala wanjala, iwo akanandidyetsa ine. Ngati ine ndikanafuna suti, iwo akanandigulira iyo. Iwo akanapita palimodzi ndi kukandigulira ine galimoto, kuti ndizilalikira Uthenga. Iwo akanandichitira chirichonse mwa njira imenyo. O Atate, fufuzani miyoyo yawo mmawa uno, chonde chitani, ndipo aloleni iwo ayifufuze iyo pamaso pa Inu. Ine sindikudziwa, ine ndikudalira kuti mmodzi aliyense wa iwo ali mwa Osankhidwa amenewo. Ndipo mundiyike ine mmenemo, inenso, Ambuye. Ndipo ngati pakhale chifukwa chirichonse mwa ine chimene ine sindikanakhala mmenemo, Ambuye, Inu mungowulula icho kwa ine, ine ndikonza icho bwino pakali pano. Ine ndikufuna kukhala wotsmikiza, Ambuye, kuti pa mmawa umenewo sipakakhala vuto ayi pa mtsinje. Ine ndikufuna kudzapita mkati tsiku limenelo. Ndipo ine sindikudziwa pamene izo ziti zidzakhale, izo zikhoza kukhalabe lero. Kotero, ndithandizeni ine kuti ndidziwe, thandizani anthu awa kuti adziwe.

¹⁶⁰ Ndipo pamene ife tiwona mitima yathu ili yosakhudziwa! O, ife timasangalala nawo Uthenga wabwino kumvetsera pa wailesi, kapena kupita ku mpingo. Ife tikuyamikira Uthenga wabwino. Ife sitisamala kuyankhula za Yesu penapake. Koma, Ambuye, liri tchimo katundu wotero kwa ife mwakuti izo zimabweretsa misonzi kwa maso athu, kuwusa moyo ndi

kulira ndi kuyima motsutsa izo, chirichonse, themberero limene likuchitidwa mu mzinda? Ambuye, mulole Mngelo wa Mulungu awone izo pa ife, ndi kutiyika ife chizindikiro. Perekani izo, Ambuye.

¹⁶¹ Ngakhale chomwecho idzani, Ambuye Yesu, tsopano ndipo mukonze mitima yathu, ndi kutipatsa ife zizindikiro Zanu zowona kuti Inu muli pakati pathu, kuti ife tikhoze kudziwa kuti ife tikulandira—tikulandira chizindikiro chotsiriza asanafike mapeto a m’badwo uno.

¹⁶² Ndipo ife tikuwona upathengo, pamene mwamuna akukhala mu fuko ndi kumakhala ndi ana obadwa mwa akazi a mwamuna wina, ndi—ndi asungwana aang’ono pa msewu, ndi mazana akukanidwa ku masukulu chaka chirichonse ndi a zaka zopitirira khumi kumakhala amayi, ndipo palibe kulemekeza, ndi momwe kuti akazi akukhala chiphe, iwoeni, mwa kusuta ndi—ndi kumwa, ndi matelevizioni ndi zina zotero zimene zikuvunditsa malingaliro a ana. O Ambuye, zingayime motalika chotani izo? Ndipo Inu, Mulungu Woyera!

¹⁶³ O Atate, ine—ine ndikumverera mwachirendo lero kuti chinachake chiyenera kuchitidwa mwamsanga, Ambuye. Ine sindikudziwa choti ndinene, koma ine ndikupemphera, Ambuye, kuti Inu muyike mu mitima yathu za choti tichite. Perekani zinthu izi, Ambuye. Ife tikupempha izo mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁶⁴ Ora liri pafupi. Munthu aliyense woganiza bwino yemwe ali nako kulingalira, akudziwa kuti chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Palibe munthu mu chipinda chino, yemwe ali nawo malingaliro ake olondola, koma yemwe akudziwa kuti dziko ili silingakhoze kuyima pansu pa zikhalidwe izi. Ife sitingakhoze kuyima, abwenzi. Palibe chinthu chimodzi, monga m’busa wanu ndi m’bale wanu, palibe chinthu chimodzi chimene ine ndingakhoze kukulondolerani inu cha iko mmawa uno koma kwa Yesu Khristu. Palibe kanthu kamene ine ndikukadziwa. Tangoganizani za zinthu zimene zaloseredwa kuti zibwere usanati Mkwatulo uchitike, chirichonse chimene ine ndikuchidziwa chakwaniritsidwa kale.

¹⁶⁵ Inu mukuti, “Bwanji za chilemba cha chirombo?” Ichochidzabwera mu Chisautso. Mpingo udzakhala utapita apo. Sadzasowa kuwayika chilemba awa, awa apita kale, mwaona. Kuyika chilemba kukuchitika tsopano. Kuyika chilemba kukusonyeza, chizindikiro. Thawirani kwa Mulungu, thawirani kwa Iye mwamsanga!

¹⁶⁶ Ine ndikudabwa mmawa uno, pamene ife tikuyembekezera pano miniti chabe. Ndipo ine ndikumverera ngati inu mukutero. Ine—ine ndikukhoza kumverera kumverera kwanu, mmodzi aliyense wa inu akuyesera kuganiza, “O Mulungu, ndifufuzeni ine!” Ndi momwe ine ndikumverera, inenso. Ine ndikuzindikira

kuti Mauthenga awa monga choncho, mzanga, si otchuka pakati pa anthu. Iwe umawatsutsa iwo ndipo iwe umats-...iwe—iwe umangowapanga iwo otsika. Winawake ayenera kuchita zimenezo. Ine ndikukhumba akadakhala mwina winawake. Koma ngati izo zikugwera ine kuti ndichite izo, ngati ine ndikusowa kuti ndikhale mkazi wokolopa, ndiroleni ine ndikolope. Ngati ine ndiri...Davide anati, “Ine kulibwino ndikhale chopondera pakhomo pa Nyumba ya Mulungu, kusiyana ndi kumakhala mu mahema ndi tchimo.” Ndiko kulondola. Chirichonse chimene Mulungu akufuna inu kuti muchite, chitani icho. Musati muchite manyazi. Ngati alipo. . .

¹⁶⁷ Ndipo, kumbukirani, ine ndikudziwa ndi chinthu chachikulu. Mukuti, “M’bale Branham, inu mukuti miyoyo isanu ndi itatu yokha ndiyoti idzapulumutsidwe?”

¹⁶⁸ Ine sindikudziwa angati ati adzapulumutsidwe, ine sindikanakhoza kukuuzani inu. Koma ine ndikunena chinthu chimodzi: iwo adzakhala apang’ono kwambiri, mu tsiku monga lino. Tangoganizani, mu tsiku lija kumene Iye analiko, ndi angati anapulumutsidwa. Taganizani za tsiku la Nowa, ndi tsiku la Loti—Loti, ndi onse amenewo, Iye anati, “Kotero izo zidzakhalanso mu kudza kwa Mwana wa munthu, chifukwa, khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza.” Inu mukuona, iwe umapita mkati mwa iwewekha, ndi Iye, ndipo ndizo zonse. Mwaona? “Ndipo koma apang’ono kumeneko adzakhhalapo amene ati adzayipeze iyo.” Ndi angati amene akukhulupirira kuti ndicho Choonadi cha Uthenga? Yesu Khristu, ananena choncho, “Apang’ono kumeneko adzakhhalapo amene ati adzayipeze iyo.” Apang’ono chabe. Mukhale mmodzi wa iwo. Ine ndikudziwa ndizo zovuta, ndicho chakhamani. Ndipo icho chikukoka pa ine kuti ndinene icho, kumverera chikondi cha munthu kwa inu, koma chikondi cha Mulungu chikundikakamiza ine kuti ndikuuzeni inu.

¹⁶⁹ Tsopano, Mzimu Woyera womwewo umene unachita mu masiku a Abrahamu, unachita mu masiku a Khristu, unalonjezedwa kuti udzakhala pano kuti udzachte chinthu chomwecho. Iye ali pano. Tsopano, ngati ine ndakuuzani inu Choonadi, Mulungu ali wokakamizidwira ku Choonadi chimenecho.

¹⁷⁰ Ngati ine sindimasunga mawu anga, ine sindine mwamuna wa mawu anga. Ngati inu simusunga mawu anu, inu sindinu mwamuna wa mawu anu. Tsopano, ine ndikhoza kukulonjezani inu chinachake ndipo ine sindikanakhoza kuchichita icho, koma—koma ine ndidzabwera ndi kukuuzani inu. Ngati ine ndiri nanu ngongole chinachake, ndi kumabisala kwa inu, ine ndine wachinyengo. Ngati ine ndibwera kudzakuuzani inu, “Ine ndiri nanu ngongole, koma ine sindingakhoze kukulipirani inu, koma ine ndichita chopambana chimene ine ndingakhoze,” ndiye inu mundikhululukira ine ndi kundithandiza ine. Mwaona?

171 Ife tonse tiri naye Mulungu ngongole chinachake. Ife tiri Naye Iye ngongole ya miyoyo yathu. Tiyeni tikhale owona mtima za iyo. Kuyenda kupitako ndi kunena. . . Musati muti, “Chabwino, tsopano yang’anani, ine ndine—ine ndine Mperesbateria. Ine ndine Mmethodisti. Ine ndine Mpetekoste. Ine ndine wa Mpingo wa Mulungu. Ine ndine Mnazirini. Ine ndine wa Pilgrim Holiness.” Musati muziganiza zimenezo! Padzakhala mamilioni a amenewo mu gehena. Inu mukhale Mkhristu, mwa Khristu.

172 Ndi angati amene akuti, “M’bale Branham, mundikumbukire ine mu pemphero tsopano, ine ndikufuna kukweza mmwamba”? Mulungu akudalitseni inu.

173 Ambuye, Inu mukuona manja awo. Ora liri pano, Mzimu Woyera wawukulu watontholetsa nyumba ino mmawa uno. Ine ndikumverera Kukhalapo Kwanu. Ine ndikuzindikira kuti Inu muli pano kuti mudzalemekeze Mawu Anu. “Ine Ambuye ndabzala, ndipo Ine ndidzatsirira iyo usana ndi usiku, kuwopa kuti ena angayikhwatule iyo kuchokera mdzanja Langa.” Inu munatumiza Mawu Anu kuti adzachite cholinga, ndipo Iwo adza—Iwo adzayenera kuchita izo, Ambuye. Lemba limanena kuti Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.

174 Iwo sakanakhoza kukhulupirira, anthu amenewo mu masiku Anu sakanakhoza kukhulupirira kuti Mzimu Woyera unali mwa Inu. Ndipo Inu munadzipanga Nokha (pokhala Munthu) Mulungu, chimene, Inu munali wobadwa kwa namwali Mwana wa Mulungu yemwe anabwera ku dziko lapansi kudzatiombola ife kuchokera ku machimo athu. Ndipo chifukwa chakuti iwo anawona Mzimu wa Mulungu mwa Inu, iwo anayesa kuwupanga iwo mosiyana. Ndipo Inu munawauza iwo, Ambuye, “Sindiri Ine ayi amene akuchita zintchitizo, ndi Atate Anga omwe akukhala mwa Ine. Iye akuchita ntchitizo. Ngati inu munamutcha Abrahamu ‘atate’ wanu. Abrahamu anawona tsiku Langa.” Zedi, iye anatero, pamene iye anali kuyima pambali pa Ine, anamuwona Iye akuchita ntchito zimenezo ndi chizindikiro. “Iye anawona tsiku Langa ndipo anakondwera.” Anati, “Inu mukulakwitsa, posalidziwa Lemba ngakhale Mphamvu ya Mulungu, momwe kuti Mulungu akanakhoza kumuphimba namwali, ndi kubala Mwana wamamuna (mwa kubadwa kwa namwali) ndi kukhala Iyemwini mu chidzalo cha Mphamvu Yake, mwa Munthu mmodzi ameneyo.”

175 Ndi momwe Iye akanakhoza kutenga Magazi omwewo kuchokera mu Thupi lija limene Iye analipereka monga Nsembe, ndi kuwayeretsa anthu kuti Iyemwini akakhoze kukhalamo, kupitiriza ntchito Yake mpaka kumapeto a chitsiriziro! O Mulungu, agalamutseni anthu kuti awone zimenezo. Perekani izi. Pulumutsani aliyense yemwe anakweza manja awo. Yeretsani mitima yawo, Ambuye, manja anga ali mmwamba. Ndiyeretseni ine, O Ambuye. Ino ndi nyumba yokonzera. Ano

ndi malo amene ife tiyenera kutsukidwa. Mulole Mzimu Woyera utisambitse ife mmawa uno, ndi kutitsuka ife kuchoka ku chivundi.

¹⁷⁶ Ife tikupemphera, Ambuye, kuti pasakhale pali munthu atachoke muno koma yemwe ati adzadzazidwe ndi Mzimu Wanu. Mwinamwake sipakhala kutengeka kumodzi kuchokera kunja pamene izo zizichitika. Koma, Ambuye, pitani mkatimo, chotsanipo chikumba ndipo tiwonetseni ife chimene ife tiri, Ambuye. Perekani izo. Ndiyeno tidzazeni ife ndi Mzimu Wanu, ndi mtima umene uli woona ndi wangwiro. Ndipo mu nthawi iyi ya kuzunzidwa ndi mayesero olimba, Inu mukule mokomera ndi mokondera kwa ife pamene ife tikuyenda motsatira, kuyembekezera tsiku limenelo. Pamene misonzi ikutsikira pansi pa masaya athu, chifukwa cha machimo a mzinda, mulole Mzimu Woyera uyang'ane pansi ndi kunena, "Apo pali mmodzi yemwe ine ndingakhoze kumuyika chilemba, iye ndi Wanga, iye ndi Wanga." Perekani izo, Ambuye. Mulole iwo apezake pakati pathu lero. Ife tikupempha izo mu Dzina la Yesu. Amen.

Pamene ndidzafika pa mtsinje pa kutha kwa tsiku,

Ndipo mphepo zotsiriza za chisoni zitawomba;
Padzakhala wina akundiyeembekeza yemwe

adzandisonyeze njira,

Sindidasowa kuwoloka Yordani ndekha.

Sindidasowa kuwoloka Yordani ndekha,

Yesu anafera machimo anga awatetezere;

Pamene ndiwona mdima, Iye

adzandiyembekezera,

Sindidasowa kuwoloka Yordani ndekha.

¹⁷⁷ Ine ndikufuna kumudziwa Iye tsopano. Tengani dzanja langa, Ambuye wofunika, nditsogolereni ine patsogolo, ndiroleni ine ndiyime. Ndiroleni ine ndiyime pano, Ambuye, motsutsa chirichonse chimene chikutchedwa cholakwika, chirichonse chimene chikuwoneka molakwika. Ine sindikusamala chimene aliyense anena, ndiroleni ine ndiyime, Ambuye. Pamene ine ndatha kuchita zonse zimene ine ndikanakhoza kuchita, ndithandizeni ine ndiyime. Tengani dzanja langa ndipo ndikokereni ine kupyola mu izo, Ambuye. Chitani chinachake, ndiroleni ine ndiyime. Pamene zinthu izo zibwera, ndi chuma cha dziko lino ndi zotukumuka zake ndi ulemerero wake; chititsani khungu maso anga kwa izo, ndiroleni ine ndizimuwona Iye yekha Amene anandifera ine. Ngati izo zinditengera bwenzi aliyense yemwe ine ndiri naye, ngati izo zitengera chirichonse chimene ine ndiri nacho; izo sizikutanthauza chinthu chimodzi, ine ndikupereka izo zonse pa guwa. Ndi zimenezo, ndiroleni ine ndiyime modzipereka. Ndipo tsiku lina pamene mpweya udzawomba mokankha pa nkhope yanga, ndipo ine ndikudziwa kuti mtima wanga wapita ndipo masiku anga atsirizidwa,

ndipo nthawi yanga yatha ndipo khadi langa latengedwa kuchokera moyikamo, ine sindikufuna kudzawoloka Yordani ndekha. Iye adzakhala pamenepo. Eya. Pamene mdima ine ndidzawuwona, Iye adzakhala akundiyembekezera ine pamenepo, ine sindidzasowa kudzawoloka Yordani ndekha. Ngati ine ndimuyimira Iye tsopano, Iye adzandiyimira ine apo. Ine ndidzakhallira moyo Iye Amene anandifera ine, moyo wanga udzakhala wokondwa bwanji ndiye. Ndimomomwe ine ndikufunira kuyima.

178 Ine ndikuganiza alipo anthu odwala pano. Kodi iye anapereka makadi aliwonse? Ine ndinayiwala. Kodi iwo anapereka makadi? Kodi paperekedwa makadi aliwonse? Aliyense amene ali ndi makadi a pemphero? Ayi.

179 Ine ndikungoyembekezera Mzimu Woyera. Ngati inu mutakhulupirira kokha, mutangokhala nacho chikhulupiriro, musati mukayike. Ngati Mulungu ati awulule kwa ine mavuto anu. . . Chirichonse chimene chiri, ine sindikudziwa; ngati inu mutakweza dzanja lanu, inu simukundidziwa ine ndipo ine sindikukudziwani inu. Ndiye ngati Mulungu ati awulule pano, kodi inu mukhulupirira kuti iye anali Mngelo yemweyo amene anabweretsa Uthenga chisanachitike kumene chiwonongeko kumbuyo uko, iye akanakhala Mngelo yemweyo amene anali kuubweretsa iwo pakali pano chisanachitike chiwonongeko china. Kodi inu mukanakhulupiririra zimenezo? Ngati inu mukanatero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Chabwino, mulole Ambuye apereke izo.

180 Iye ali pafupi kwa ine. Pali mmodzi wina yemwe wakhala pafupi ndi ine, pali Akazi a Snyder pano, kapena kodi awa ndi Akazi a Murphy pano, dzina lawo ndi ndani, akhala pano pomwe. Ine ndikuwadziwa iwo.

181 Ine sindikumudziwa bambo uyu, iye ndi mlendo kwa ine. Koma Mulungu akumudziwa iye. Ngati Mulungu ati awulule izo tsopano, ndi angati a inu amene mukudziwa kuti izo siziri.

182 Tsopano, musati muyang'ane pa ine. Mai, ine ndine wa chi Kentucky namlomo wakuphiri, monga ine ndikukhudzidwira. Ine—ine ndiribe ngakhale maphunziro okwanira, nkomwe, kuti—kuti ndilembe dzina langa lomwe. Koma pali chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa, ine ndikumudziwa Iye. Ndipo kuti, ndizo—ndizo zonse zimene ine ndikusamala kuti ndizidziwe. Tsopano, musati—musati mupereke chidwi chirichonse ku chimene galamala yanga ili.

183 Ndipo inu mukhoza kuganiza kuti Ulaliki wanga mmawa uno unali wonse kunjira kwa mzere ndi chirichonse, inu muwufoletse iwo ndi Baibulo nthawi imodzi ndi muwone ngati inu simuli kumene pa chandamale cha ziro. Muwone ngati choyang'anira chanu sichiri mkati pamene inu—pamene inu muchiyike icho pamenepo. Musati mufoletse izo ndi

malingaliro anu anu, koma muchifoletse icho ndi chimene Iye anati. “Khwalala ndiro chipata, njirayo ndi yopapatiza, ndipo apang’ono kumeneko adzakhhalapo amene ati adzayipeze iyo; chifukwa njirayo ndi yotakata imene ikutsogolera ku ziwonongeko, ndipo chipata ndi chachikulu, ndipo ambiri adzalowa mkati pamenepo,” mamiloni kuchulukitsa mamiloni adzalowa mkati pamenepo. Mmodzi kuchokera mu milioni mwina zidzakhala momwe izo zidzabwerere. Apo inu muli. Ndizo zimene Iye ananena. Tsopano, Iye sanapereke chiwerengero chimenecho, koma Iye anati, “Monga izo zinali mu masiku a Nowa, miyoyo isanu ndi itatu. Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, itatu.” Kuchokera mwa chinthu chonsecho, atatu anapulumsidwa ndi moto. Chotero izo zidzakhala!

¹⁸⁴ Tsopano, ngati aliylene ali wauzimu kwenikweni, ine ndikufuna inu muyang’ane pa munthu uyu wakhala apayu, iye akundiyang’ana ine mowirikiza basi monga iye angathere. Anakweza mmwamba dzanja lake, ine sindikumudziwa iye; sindinamuwonapo iye, ndipo ine sindikudziwa kanthu za iye. Iye wangokhala pamenepo akuyang’ana pa ine. Koma, onani, iye akupanga kukhudza, iye akupemphera. Tsopano, ndiko kulondola. Tsopano, ngati Ambuye ati andiuze ine. . . Munthu uyo atakhala patali chotero kuchokera kwa ine, ndipo uku ndi kukomana kwathu koyamba, ndipo apo iye wakhala pamenepo. Ngati Ambuye ati awulule kwa ine chimene iye ali—chimene iye ali. . . ine—ine sindikanakhoza kumuchiza iye, ine sinditero, ine sindikanakhoza kuchita izo, chifukwa Mulungu anachita kale izo. Koma izo zikanawonjezera chikhulupiriro chanu. Aliyense akuwona tsopano, Iye ali pomwe pano, basi Mzimu womwewo. Ndipo kumbukirani, Yesu analonjeza izi, isanafike nthawi yotsiriza. Icho nthawizonse chakhala chizindikiro chotsiriza.

¹⁸⁵ Tsiku lina, Leo ndi ine tinali titakhala pa msewu, ndipo ena a ife tikuyankhula. Ndipo ine ndimapitirira kumverera kuti pali kusintha kukubwera, kusintha kukubwera. Pamene ife tinayankhula za iko, iko sikukhala kusintha mu utumiki wanga, chifukwa iko sikungakhoze kukhala kwinanso, koma iko kudzakhala kusintha mwa ine. Ine nthawizonse ndakhala wofooka ndi kumangolola anthu azinditsogolera ine ndi kumandilondolera ine, ndi kundituma njira *iyi* ndi njira *iyoyi*. Ngati ine ndikanachita chinachake chimene Ambuye anandiuza ine kuti ndizichita nthawi yayitali kale, ine sindikanakhala mu vuto limene ine ndirimo lero. Ine ndikupita kunja sabata lotsatira ili kuti ndikakhale ndekha ndi Mulungu. Inde, bwana. Ine—ine ndiyenera kumvetsa kuchokera Kumwamba. Ine sindikufuna kukhala wofooka, ine ndikufuna kuyima pa kukhudzidwa kwanga komwe.

¹⁸⁶ Bamboyo, izo zikupitirira kubwerera kumbuyo komwe kwa iye, iye wakhala kumbuyo komwe, chifukwa munthu ameneyo akukhulupirira, iye akukhulupirira kwenikweni.

Ine ndikupenya omvetsera paliponse, ndipo iko kukugwera molunjika kumbuyo komwe kwa bamboyo. Iye ali nacho chosowa, iye ali wolemedwa, koma iye ali wolemedwa chifukwa cha winawake. Ndiko kulondola. Inu mukupempherera winawake. Inu muli naye winawake pa mtima wanu. Ndiko kulondola, sichoncho? Ndi mzanu. Ngati ine ndingakuuzeni inu limene liri vuto ndi mzanu ameneyo, kodi inu mundikhulupirira ine kukhala wantchito wa Mulungu? Ndi uchidakhwa. Ndiko kulondola. Ngati ndiko kulondola, kwezerani mmwamba dzanja lanu.

¹⁸⁷ Kodi inu mukukhulupirira? Winawake cha apa anakweza dzanja lawo, mkazi kumbuyo kuno, winawake. Inde. Eya. Inu simukundidziwa ine? Ine ndine mlendo kwa inu nonse? Ine sindikukudziwani inu, koma Mulungu akukudziwani inu. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ngati Mulungu ati awulule kwa ine chomwe chiri pa mtima wanu, kodi inu mundikhulupirira ine kuti ndi wantchito Wake? Dona wamng'ono, chomwe inu mukuvutikana nacho ndi mwana uyo pamenepo. Ndiko kulondola. Ndipo mwana ameneyo ali ndi chikanga pa nkhope yake. Adotolo sangakhoze kuchita kanthu za izo. Ndinu mlendo kuno, ndipo inu ndi wokonedwa wanu wakhala pamenepoyo. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu angakhoze kundiuza ine yemwe inu muli kapena kumene inu mukuchokera? Inu mukukhulupirira izo? Kodi inu muvomereza machiritso a mwanayo ngati Iye angatero? [Dona akuti, "Inde"—Mkonzi.] Chabwino, inu mukhoza kubwerera ku Somerset, Kentucky, kumene inu mwachokerako. Ndipo khulupirirani kuti iye akhala bwino, chikanga chimusiya mwanayo ngati inu mungakhoze kukhulupirira izo.

¹⁸⁸ Pamene ine ndinatchula mawu amenewo, winawake wayima kumbuyo uko mu holo, wochokera ku Somerset, Kentucky, akupemphera, ali ndi vuto la mtima. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwapanga iwo kukhala bwino? Ngati inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, ndi khulupirirani kuti Mulungu akuchizani ndi kukupangani kukhala bwino.

¹⁸⁹ Kuno, kuno kuli, ine ndikukhulupirira kuti dzanja la winawake linabwera mmwamba kumene motsatira kuno, motsatira kumene, dona. Eya, ine ndinawona dzanja lanu. Kodi ndine mlendo kwa inu, dona? Ine sindikukudziwani inu. Ife sitinayambe takomanapo. Kodi inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake? [Dona akuti, "Inde"—Mkonzi.] Inu mukutero? Inu muli ndi cholemetsa pa mtima wanu, kapena chinachake. Inu mukukhulupirira kuti ngati Mulungu angakhoze kuwulula izo kwa ine, inu mukukhulupirira kuti Ndiwo Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu? Mwamuna wanu wakhala apoyo, iye akukhulupirira chinthu chomwecho, nayenso? Kodi inu mungakhulupirire chinthu chomwecho? Ndi zokhudza msungwana wanu wamng'ono wakhala pafupi ndi inu

pamenepoyo. Ndiko kulondola, iye ali ndi khansara. Koma kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amuchiza iye? Ngati inu mukutero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, ikani manja anu pa mwanayo.

¹⁹⁰ Ambuye Yesu, mu Kukhalapo kwa Mzimu Wanu, ine ndikutsutsa mdierekezi yemwe akumupha mwanayo. Ine ndikuyika, mwa chikhulupiriro, Magazi a Yesu Khristu pakati pa wakuphayo ndi mwanayo. Mulole iye akhale moyo. Amenii.

¹⁹¹ Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musati mukayikire. “Ngati inu mungati mukhulupirire, zinthu zonse ndi zotheke.” Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheke. Kukhoza.

¹⁹² Wina wakenso kumbuyo kumeneko anakweza dzanja lawo, penapake, inu, dona cha pamapeto. Inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito wa Mulungu? Ine sindikukudziwani inu, inu simukundidziwa ine. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu angakhoze kuwulula kwa ine chomwe chiri vuto lanu? Kodi inu mukanati mumuvomereze Yesu kuti akhale Mchiritsi wanu kapena Wopereka, chirichonse chimene chiri, chirichonse chimene icho chiri. Inu mukukhulupirira izo ndiye? Chabwino, ndiye kusweka kwamanjenje uko kumene inu munali nako, ndi chimene inu munali nacho. Ngati ndiko kulondola, imirirani pa mapazi anu, ngati ndiko kulondola, basi kuti anthu awone kuti ndi zoonu. Chabwino, izo zikuchokerani inu tsopano. Inu mupita kwanu ndi kukakhala wabwino. Mulungu akudalitseni inu.

Ndinu wochokera ku Kentucky, inunso. U-nhu, ndiko kulondola.

¹⁹³ Dona wakhala pafupi ndi inu ndi wochokera ku Kentucky, nayenso. Iye ali, nayenso. Ine sindikukudziwani inu, kodi ine ndikukudziwani? Koma ine ndingakhoze kukuuzani inu kuti muli ndi chinachake cholakwika ndi inu. Ngati ine ndingakhoze kukuuzani inu chimene chalakwika ndi inu, mumulandira Khristu ngati Mchiritsi wanu? Ichu chiri mchiunu mwanu. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, mokweza pamwamba koteru kuti anthu akhoze kuwona. Chabwino, pitani kwanu tsopano, ichu chikusiyani inu. Chikhulupiriro chanu chikupangitsani inu kukhala bwino.

Ine ndikutsutsa inu kuti mukhulupirire. Ine ndikutsutsa chikhulupiriro chanu kuti mukhulupirire.

¹⁹⁴ Pano pakhala dona pano, akupemphera, wakwezera mpango wake mmwamba ku nkhope yake. Ine sindikukudziwani inu. Mulungu akukudziwani inu. Ndinu wochokera ku Joliet, Illinois, ndipo inu muli ndi chotupa. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Inu mukhoza kudabwa... (Inde, ndi m—ndi mkazi amene Rosella anamubweretsa. Ndiko kulondola. Dikirani, iye anandiuzana ine za izo, koma iye sanadziwe konse izo ine sindimamudziwa konse mkaziyo. Ndiko

kulondola. Zangopezeka kuti chikhulupiriro cha mkaziyo chinali chachikulu.) Ine ndikuuzani inu chinthu chimodzi—inu mukudziwa kuti ine sindikuchidziwa. Inu mukupempherera mwana uyu wakhala apayu pa mapeto a mpando, yemwe akudwala. Uyo ndi mwana wanu. Ndiko kulondola. Ameni. Inu mumadziwa kuti ine sindimadziwa zimenezo.

¹⁹⁵ Apo Iwo uli, Ndi Mzimu Woyera! Kodi inu mukuwukhulupirira Iwo? Kodi inu mukuwuvomereza Iwo? Ndiye ngati ndiko kulondola, zimene ine ndinanena za “khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza” ndi zolondola. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ali pano pomwe tsopano. Mzimu wa Mulungu wamoyo uli pano pomwe. Kodi inu mukuwukhulupirira Iwo? Ndiye, kuti ndikuloleni inu kuti mudziwe kuti ine sindine winawake woti ndikuchizeni, ine si mchiritsi, koma Mzimu wa Mulungu unangondisankha ine kuti ukadziwonetsere Wokha. Ine ndiribe maphunziro ayi. Ine ndiribe chidziwitso cha chirichonse. Koma ndi Mzimu Wake umene umachita zimenezo, inu mukuona, ndipo Iye akufuna kuti inu mudziwe kuti ine ndakuuzani inu Choonadi.

¹⁹⁶ Ichi ndi Choonadi, kuti Yesu Khristu akupangitsa mmodzi aliyene wa inu kukhala bwino pakali pano ngati inu muti mukhulupirire izo. Tsopano basi monga . . . Ngati izo zinagwira ntchito mu Kingston, zimene amishonare, kapena aliwonse amene ali kumbuyo uko, anawuwona Iwo ukugwira ntchito mu Kingston, mwa zikwi ziri kuchizidwa, bwanji kuti Iwo usagwire ntchito mu Amerika muno kumene ife tiri nazo momwe izo ziyenera kukhalira. Chifukwa chiyani kuti ife sitingakhoze kukhulupirira izo? Chifukwa ife sitingakhoze kuwoloka mathithi aang’ono awo kutsidyako. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Kwezerani mmwamba manja anu.

¹⁹⁷ Tsopano, manja omwewo ayikeni pa winawake pafupi ndi inu, ndiroleni ine ndimupempherere iye kuchokera pomwe pano, ndipo musati inu mukhale ndi kukayika kwinanso mu mtima wanu, izi zithetsa izo.

¹⁹⁸ O, mai, M’bale Neville! Momwe ine ndakhumbira, momwe ine ndapempherera, momwe ine . . . Inu mukhoza kuganiza kuti ine ndapenga; ine sindiri. Ine ndikudziwa kumene pamene ine ndiri. Ngati ine ndikanakhoza kokha kutengera kanthu kakang’ono aka kwa inu! Kodi inu mukuzindikira kuti Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, pano pakati pa anthu mmawa uno, pakali pano, alipo pakali pano, akudzisonyeza Iyeyekha?

Chabwino, inu mukuti, “M’bale Branham, *inu* munanena izo.”

¹⁹⁹ Ine ndinanena motani izo? Ine sindikukudziwani inu. Alipo mkazi wina ali ndi TB. Inu mwachiritsidwa, mlongo. Akudalitseni inu. Ine ndikupempha kukhululukira kwanu, inu munali kumupempherera mkazi wa TB, chifukwa ndi mkazi wa

tsitsi lotuwa. Eya. Chabwino, khulupirani izo. Chabwino. Iye ali pano. Ndiko Kukhalapo Kwake.

²⁰⁰ Tsopano, pano pali zimene Iye ananena, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akukhulupirira. Ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Iye angakhoze bwanji kunama? Mwaona, izo siziri pa Iye, izo siziri pa ine, tsopano izo ziri pa inu. Tsopano inu mukhulupirire.

²⁰¹ Ine ndikuyang’ana pa mkazi wamng’ono wakhala kumbuyo uko pakali pano, iye ali ndi chikhulupiro chochuluka. Iye ndi mwamuna wake angobwera mwatsopano kwa Ambuye. Iye ali mu msonkhano uno womwe, anali ndi chophuka chimene adokotala amati akang’ambe pa iye basi asanati, ndipo pamene mwana wake amakonzekera kuti abadwe. Ndipo adokotala anali oti akamung’ambe pambuyo pake, koma mwanayo anabadwa ndipo sakukhoza kupeza chophukacho panonso. Icho chonse chapita. Mukuona? Chifukwa chiyani? Iye anangokhala monga... Iye sanali kuno pa nsanja monga choncho. Iye anangokhala kumbuyo uko ndipo anakhulupirira izo. Nkulondola uko, Akazi a Green, ine ndikukhulupirira iwo ali, kumbuyo uko? Ndiko kulondola. Mukuona dzanja lawo? Adokotala sakukhoza kupeza ngakhale chophukacho, icho chonse chapita. Chifukwa chiyani? Iye anakhulupirira izo, anangotuluka panja ndi kunena, “Ndi zolondola!”

²⁰² Tsopano inu muchite zomwezo, ndipo kusautsika kulikonse kumene inu muli nako kuyenera kuti kuchoke. Mulungu, Ndani angakhoze—Ndani angakhoze kutumiza Chinachake kulowa mu thupi la munthu, kupita mu malodza a kuluma kwa njoka ija imene inali mu phazi la munthu uja, kupereka chiphe, kuti chimuphe iye, ndipo akhoza kuyimitsa izo ndi kuchipha icho apo pomwe, ndi mochuluka bwanji momwe Iye angakhoze kuphera matenda mu thupi lanu. Chifukwa, munthu ameneyo anali mu kusautsika ndipo iye amayenera kuti akhale ndi thandizo. Inu muyenera kutero, inunso. Ngati inu simukhala nalo, inu mufa.

²⁰³ Tsopano manja anu akhalebe pa wina ndi mzake. Musati mudzipempherere nokha, inu mumupempherere munthu pafupi ndi inu. Ndizo monga—Mkhristu.

²⁰⁴ Phunzirani ichi, phunzirani ichi, kuti, momwe inu muchitira kwa ena, inu mukuchita kwa Khristu. Pamene inu mukhala wabwino kwa winawake, inu mukukhala wabwino kwa Khristu. Ngati iwe umuzunza winawake, iwe ukumuzunza Khristu. O, mai!

²⁰⁵ O, ngati ine ndikanakhoza kokha kutenga izi kuti zikhale zitawafikira, ngati ine ndikanakhoza chabe kuwalola anthu kuwona izi, chimene ine ndikuyang’anapo ndi chimene ine ndikumverera, ndi chimene ine ndikudziwa kuti chiri kuchitika pano, onani. Momwe Khristu akukankhira utatha Uthenga uja mmawa uno, kuti ufike pansí kumene ulowe mu mitima ya

anthu ndi kulenga chinachake mmenemo; osati chokondweretsa, osati chotengeka (izo zimabwera ndi icho), koma kuti chilenge chikhulupiriro chosafa mmenemo chimene sichiti chinene, kupereka inchi kwa mdani.

²⁰⁶ Tsopano, Iye amva pemphero langa, Iye amva lanu. Inu mupemphererane wina ndi mzake tsopano, pamene ine ndikupempherera nonse a inu.

²⁰⁷ O Ambuye, mphindi yayikulu yovuta iyi, ife tikuzindikira kuti izi zitanthauza kusiyana pakati pa imfa ndi moyo, kwa ambiri. Ndipo ine ndikunjenjemera mu Kukhalapo Kwanu, chifukwa ine ndikudziwa, Ambuye Mulungu, kuti ine ndiyenera kupemphera ndi mtima wanga wonse. Ine ndikuzindikira kuti ngakhale kuti pakhoza kusakhala munthu wodwala pakati pathu mu maminiti ena asanu, kuti munthu aliyense muno adzazindikire kuti Inu muli pano. Pano iwo akuyima mmawa uno, Ambuye. Aloleni anthu amenewo akwezere mmwamba manja awo amene amadziwa kuti ine sindiri kuwadziwa iwo, ndi popanda kanthu za iwo. Koma Mzimu Wanu ukuwadziwa iwo. Inu mukudziwa chinsinsi cha mitima yawo, ndi mochuluka bwanji momwe Inu mukudziwira zosautsa zawo ndi kuvutika kwawo! Ndiye, Ambuye, mulole izo zikhale lero, mulole izo zikhale ngakhale pano kuti Mzimu Wanu udzawakhudze matupi awo odwala. Perekani izo, Ambuye. Iwo akupemphererana wina ndi mzake.

²⁰⁸ Ndipo ine ndikupemphera, Wokondedwa Mulungu, kuti Mzimu Woyera udzapangitse izo kwenikweni kwambiri kwa iwo, kuti iwo asati adzakayikire izo kachiwiri. Ndipo alipo matenda ena, Ambuye, amene ali aakulu kwambiri kuposa matenda athupi awa, ali matenda auzimu. Mulole mtima uliwonse utsegulidwe.

²⁰⁹ Ambuye, izo zingakhoze kukhala motani kuti Inu munayima pamenepo pa mbali ya Abrahamu, ndipo munachita chinthu chomwechi, munamuza Sarah yemwe anali “kuseri” kwa Inu, Lemba limatero, “mu hema iye anaseka,” ndipo Inu munamuza iye. Ndipo Abrahamu anzindikira kuti ameneyo anali Elohim, Mulungu wamkulu. Mu maminiti pang’ono Inu munali mutasowa pamaso pake.

²¹⁰ Ndipo, Ambuye, pamene Yesu anayima ndipo anachita chinthu chomwecho, ndipo anati, “Inu munamutcha Abrahamu ‘atate’ wanu, ndipobe inu mukunena kuti inu mukuwadziwa Malemba.” Anati, “Inu mukulakwitsa, posawadziwa Malemba ngakhale Mphamvu ya Mulungu.” Ndipo iwo anamutcha Iye “Belezebule.”

²¹¹ Koma inu munalonjeza kuti mu masiku otsiriza kuti Inu mukanadzatsanulira Mzimu Wanu Kachiwiri. Mneneri anati, “Mu nthawi yamadzulo kudzakhala kuli Kuwala.” Ndipo ndi ife pano.

²¹² Pamene dziko lapathengo ili likuzezedeka pansi pa tchimo, monga munthu woledzera akuzandima kupita kwawo usiku, posakhalitsa lidzaphulitsidwa pakati pake, sipadzakhala pali ngakhale fumbi la phala lamoto, nkomwe, lotsalira la ilo. Ndipo ife tikuwona nthawi ikugunda chopita.

²¹³ O Mulungu, chotsani kukayikira kulikonse kuchokera kwa ife. Tisunthireni ife kulowa mu mkombero umenewo pakali pano. Bwerani, Mzimu Woyera. Gwirizirani mapiko Anu aakulu, fungatirani pa omvera apang'ono a anthu awa pakali pano, ndipo dziloleni Inunokha kolowerera mu mitima yawo, ndipo aloleni iwo adziwe kuti Inu muli mu Kukhalapo Kwauzimu, kuti ndi Inuyo, “Ine ndine Ambuye Amene amachiza matenda anu onse.” Ndipo mulole Kukhalapo Kwanu kuchite chinachake kwa mtima wawo chimene chiti chidzawapangitse iwo kupita pochoka pano, mmawa uno, akukhulupirira ndi zonse zimene ziri mwa iwo. Ndipo mulole munthu aliyense wodwala ndi wosautsika achizidwe.

²¹⁴ Pakuti, monga wantchito Wanu, ine ndikuyima ndi kutsutsa mdierekezi aliyense, kutsutsa matenda, kutsutsa Satana.

²¹⁵ Iwe waluza, ndipo sindiwe kanthu koma chonyenga. Ndipo ife tikuyitanitsa dzanja lako pamenepo mmawa uno, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo monga wantchito Wake, kulalikira Mawu Ake ndi kuwauza anthu Choonadi, kuti iwo akhale oyanjana ndi kufola ndi Mawu a Mulungu, ine ndikukudzudzula iwe, Satana, mu Dzina la Yesu Khristu. Choka kwa mmodzi aliyense wa anthu awa amene abwera kuchokera kutali ndi pafupi, kuti adzachiritsidwe. Iwe uchoke pa omvera awa ndi pa anthu awa. Ine ndikukulumulira iwe mwa Mulungu wamoyo. Ndipo Baibulo linati, “Pemphero loona, lamphamvu la munthu wolungama lidzapambana kwakukulu.” Ndipo anthu ambiri olungama ali ndi manja awo atayikidwa pa odwala, mmawa uno. O, Satana, iwe ukanafuna kuwafikitsa iwo poganiza kuti izo anali ine, ndiye iwe ukutenga ulemereko kuchokera kwa iwo. Koma ndi chikhulupiriro chawo mwa Mulungu, naponso, iwo akukhulupirira Mulungu! Ndipo iwe uyenera kuti usunthe, mwa chikhulupiriro chawo. Kotero tenga ulendo wako uchoke pano, ndipo pita ku mdima wakunja kumene kuli kwa iwe. Ine ndikukutsutsa iwe, mu Dzina la Yesu Khristu, mwa ulamuliro wa Baibulo la Mulungu, utumiki wanga mwa Mngelo. Tsopano pita, mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo alole iwo akhale afulu. Amen.

²¹⁶ Kodi inu mukukhulupirira, mitima yanu yonse, kuti inu mwachizidwa? Kwezani dzanja lanu, nenani, “Ine tsopano ndikumulandira Yesu Khristu monga Mchiritsi wanga. Mithunzi yonse yachoka kuchoka kwa ine. Ine tsopano ndikumulandira Iye mu chidzalo cha mphamvu Yake, mu kudala kwa Kukhalapo Kwake. Ine ndikumuvomera Iye.”

Chikhulupiriro changa chikuyang'ana kwa
 Inu,
 Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
 Mpulumutsi wauzimu;
 Ndimvereni pamene ndikupemphera,
 Tengerani machimo anga kutali,
 Musandirole ine kusochera
 Kuchokera ku mbali Yanu.

Tsopano tiyeni tikweze manja athu mokoma kwenikweni
 kwa Iye tsopano.

Pamene njira ya mdima ndikuyenda,
 Ndi zodandaulitsa ziri pozungulira ine,
 Khalani Namulondolera wanga, O Mulungu;
 Thamangitsani mdima ukhale usana,
 Pukutani zisoni, mantha achoke,
 Musandirole ine kusochera
 Kuchokera ku mbali Yanu.

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza "Chikhulupiriro
 Changa Chikuyang'ana Mmwamba Kwa Inu."—Mkonzi.]...
 chisomo cholemera!



Mpingo Ndi Chikhalidwe Chake
(*The Church And Its Condition*)
Ogasiti 5, 1956, Lamlungu Mmawa

Khwalala Ndiro Chipata
(*Strait Is The Gate*)
Marichi 1, 1959, Lamlungu Mmawa

Mpingo Wonyengedwa Ndi Dziko
(*A Deceived Church, By The World*)
Juni 28, 1959, Lamlungu Mmawa

Mauthenga awa a M'bale William Marrison Branham, anaperekedwa pachiyambi mu Chingerezi ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., atengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anasindikizidwa mu Chingelezi. Maulaliki awa anamasuliridwa mu Chichewa ndi kudindidwa mu 1997 ndi:

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org